


MAFUNSO NDI MAYANKHO

AHEBRI, GAWO I

 Iye akanakhoza bwanji kuchita izo popanda Mulungu? Ilo likanakhala liri lenilenilo, si choncho? Sizikanakhoza kuchitidwa popanda Ambuye.

Ine sinditi ndilalikire kuchokera mwa izo zonse. Koma ine ndinaganiza kuti zikanakhoza kugwira chinachake kukhala ngati molemera, inu mukudziwa, kotero ine ndibwino ndikhale wokonzekera. Koma, o, izo zinali, zopepuka kwambirimбири. Chotero mwinamwake palibe mafunso ochuluka kwambiri pakati pa anthu ndiye, ndi mafunso basi ophweka ndi opepuka. Chabwino, ndine wokondwa kuti ndiyesere kuwayankha iwo mwakukhoza komwe ine ndingathere, mwa kuthandizidwa ndi Ambuye.

² Ndipo ngati Mlongo Arganbright ali muno usikuuno... Mlongo Ruth. Kodi inu muli muno, Mlongo Ruth? Cha kuno. Ine ndiri... O, inde, ine ndiri nayo adiresiyo pano, ndi... Ayi, ine ndiribe. Chabwino, ine ndikhoza kuipeza iyo pomwe pano. Ine ndinali nayo iyo mu bukhu la mthumba mwanga, ndipo ine ndalisiya bukhu lamthumba langalo kunyumba. Tsopano, ngati apolisi andigwira ine popita kunyumba, M'bale Fleeman, inu mubwere pondiwombola ine. Muuzeni Billy ine ndi... ndasiya bukhu langa la mthumba kunyumba, ine ndikuyendetsa wopanda laiseni usikuuno. Ine ndimaganiza kuti ndinali nalo ilo mthumba mwanga; ine ndinangosintha zovala. Ine ndinathamanga kukalowamo, madzulo ano, ndinali ndikudula udzu mofulumira kwambiri ndipo ndinayenera kusiya ndi kufulumira nkukasintho zovala ndi kuthamanga kubwera kuno. Ndipo i—ine ndinaibweretsa lexicon, koma inu mukhoza kuitenga iyo kenako basi kuchokera mmenemo.

³ Musamverere nayo moyipa kalata *imeneyo*. Ngati ine ndikanakhala kuti sindinalandirepo ina yoipa kuposa iyo, iyo ikanakhala ili kalata yabwino. Iyo inali yabwino. Iyo inali y—yabwino kwambirimбири. Ine ndinakuuzani inu kuti ine sindikanati ndiiwerenge iyo, koma ine ndinasuzumira pa iyo, inu mukudziwa, ndipo sindikanakhoza basi kuzigwira mwa kutalika kwinanso. Ine ndimangodabwa zomwe iye ananena. Ndipo iyo inali y—yabwino kwambirimбири, analemba momwe mphunzitsi weniweni wa sukulu amayenera kuti azilemba. Izo zinali zabwino, ndipo ine ndikuziyamikira izo. Ndipo i—izo zikundipatsa ine... .

⁴ Inu mukuona, ine ndimakonda makalata a winawake yemwe angati—yemwe angatsutsane pang’ono ndi iwe. Mwaona, ngati iwe izingopita limodzi nawo nthawi zonse, popanda wina wotsutsana nawe, iwe umaduma. Iwe umayenera kuti uzipeza zokutsutsa pang’ono kuti iwe uzikhoza kumamvetisa ndi kukumba pansi. N—ndipo iwe umangolowa mu kachitidwe kamodzi ngati sungasamalire; ndiye iwe—ndiye iwe umalowa mu vuto pamene iwe uchita izo. Iwe umayenera kuti uzikhala ngati ukupitirira kusunthira mtsogolo ndi kupeza winawake yemwe akutsutsana nawe ndi kukufwanyula nthenga zako kamodzi mu kanthawi.

⁵ Uko ku Afrika ine ndinapezako mikango iwiri yaing’ono, ndipo iyo inali tinthu tating’ono kwambiri, pafupi monga *choncho*. Tamangamanga, tating’ono, mkango waung’ono kwambiri; mkango wawung’ono, mkango waung’ono waukazi. Ndipo tsopano, iyo inkawoneka ngati tiamphaka, iyo inali yaing’ono kwambiri monga *choncho*, yaing’ono...tinthu tating’ono tokongola kwambiri, iyo inali ikungosewera. Ine ndinkati ndiibweretsa iyo ku Amereka, ine ndinali nayo iyo mu khola la mbalame. Ine ndinkati ndiibweretse iyo pobwerera, koma ine sindinakhoze kupeza chiri—chirichonse choti ndiipatse iyo katemela, mankhwala aliwonse. Ndipo iwo sakanandilola ine kuti ndiibweretse iyo mu United States popanda iyo kupatsidwa katemela choyamba, ndipo ine sindinakhoze kumupeza iye mu Afrika yense. Koma ngati iwe umafuna kuti udziwe ngati uwo unali mkango kapena ayi, ungomukandira iye chammbuyo pang’ono pokha. Iye angadzifunzulule ndi kukulola iwe kuti udziwe kuti iye ndi mkango, ch—chotero izo zimakhala ngati zimakudziwitsa iwe pamene iye waima.

⁶ Umo ndi momwe iwe umayenera kuti uzichitira kamodzi pa nthawi, inu mukudziwa, kukhala ngati kufwanyulira nthenga chammbuyo, kuti upeze. Koma, tsopano, ife sitimakwiya ngati mkango; ife basi—ife timangozikonda izo, ku...anthu kuti azitifunsa mafunso. Ndipo mafunso onga awo, Mlongo Ruth, ndi a—abwino, kwambirimbiri kwa ine. Ndizo...i—ine ndimazikonda izo, mwaona. Ndi a mtundu wonyansa kwenikweni aja omwe ine ndimadana nawo kuti ndi watenge. Koma awo...izo zinali zabwino.

⁷ Tsopano ife tiri nawo ena okondoweza, abwino, basi mafunso akwathu. Kuli mlaliki kumbuyo uko mu chipinda chakumbuyocho tsopano pompa, anandifunsa ine, anati, “Aneneri awiri a Chivumbulutso 11, kodi iwo adzabwera umo usanachitike Mkwatulo? Kapena basi asanati awachotsepo Aisraeli? Ndipo nchiani...” Tsopano, uwo ndiwo mtundu wa mafunso o—o—omwe amakumanga mokuzengeza. Koma mafunso ophweka awa ngati ili ndi abwino bwino.

Koma tsopano, ife tisanayambe, tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa pemphero:

⁸ Atate, izo zadziwidwa kuti pamene Inu munali usinkhu wa zaka thwelofu, Inu munapezedwa mu Kachisi muli ndi alembi ndi aluntha, mukukambirana nawo Malemba. Ndipo iwo anali—iwo anadodometsedwa pa . . . amuna achikulire, ndi ophunzitsidwa bwino mu Malemba, ndipo komabe kumuwona mnyamata wamng’ono wa pafupi usinkhu wa zaka thwelofu basi akungo—akungowadodometsa, mu kufotokoza kwa Malemba. Inu munali pa ntchito ya Atate Anu. Inu munanena kwa amayi Anu, “Kodi inu simukudziwa kuti Ine ndiyenera kuti ndizikhala pa ntchito ya Atate Anga?” kuti ndizifotokoza Malemba ndi matanthauzo ake auzimu?”

⁹ Ndipo tsopano ife tikupemphera, Ambuye, k—kuti Inu podziwa momwe ife tiriri ofooka ndi olobodoka, ndi momwe ife timakhozera kulakwitsa, kuti Inu mungobwera nafe usikuuno mu maonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo mudzalongosolere Malemba kwa ife. Ine ndikuyembekezera ndi kudalira pa Inu. Ndipo ngati ine ndingadzati konse, pa nthawi iliyonse, kuyesera kuti ndiike malingaliro anga anga kapena kutanthauzira kapena chinthu china modzikonda, kuti ndiyesere kuzipanga izo kuti zimveke ngati momwe ine ndimazilongosolera kuti izo zikanakhala ziri zolondola, muiteke kamwa yanga, Ambuye, monga momwe Inu mukana . . . Inu munachitira ndi mikango, pamene iyo inkadza kwa Daniele. Inu mukadali Mulungu yemweyo.

¹⁰ Ndipo lolani izo kuti zikhale kwathunthu . . . Pamene ife tikudalira pa Mzimu Woyera, mulole Iye angoziwululira zinthu izi kwa ife. Ndiyeno pamene Iye aziyankhula izo, azipange izo momveka kwambiri kuti yemwe anafunsa funsola akhoze kuzilandira Izo. Ndipo ngati Izo ziyankhidwa mosiyana ndi zomwe ine ndakhala nthawizonse ndikuzikhulupirira, ndiye mulole mtima wanga usangalale nawonso, Ambuye, podziwa kuti ndapeza chinachake chatsopano, ndi njira yina yabwino ya Ambuye. Pakuti Inu munati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo iwo ndi omwe amachitira umboni za Ine.”

¹¹ Tsopano, kukatha kuphunzitsa kwa Lemba uku, iko ndithudi kuutsa malingaliro ambiri ndi zina zotero. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, tsopano kuti mafunso onse awa akuwoneka kuti afunsidwa mokoma ndi modekha kwambiri, mulole Mzimu Woyera modekha ndi mokoma uwayankhe iwo. Pakuti ife tikupempha izo mu Dzina la Yesu, ndi kwa ulemmero wa Mulungu, ndi kwa kumanga mokuza kwa Mpingo Wake kuti ukule. Amen.

¹² Pali nthawi zambiri pomwe zolinga zakudzikonda pa chirichonse, kumangowononga kukoma konse kwa icho. Ndipo tsopano, mafunso pambuyo pa Lemba ili afunsidwa kale.

¹³ Tsopano, ngati ine ndiziuzira pang'ono pokha usikuuno, ine ndazula dzino. Ndipo ine ndikaikapo ilo, ndipo ine sindikutha kumalalikira, ine ndikumachedwetsa pamene ine ndikulalikira; ine ndikalichotsapo ilo, ndipo ndikumakhala pafupi kuimba muluzi.

¹⁴ Akazi a Billy Graham ananena nkhani ya iye, kuti kutengeka koipa komwe iye anayamba amuwonapo iye, kunali, iye atagulula dzino patsogolo. Ndipo iye analitaya ilo, ndipo iye anali ndi programu ya pa televizioni nthawi yomweyo, n—ndipo iye sankakhoza. . . Ilo linali pa mbale ndi mano ena akumbuyo mu iyo. Ndipo pamene iye ankati ayankhule, iye ankayimba muluzi “psyfuu, psyfuu” kupyolera pa dzino lakelo. Ndipo iye anatani iye anali pansu pa maondo ake, akupemphera ndi kuchita thukuta, maminiti khumi asanayambe kuwonetsa pa televizioni, ndipo potsiriza iwo analipeza ilo pamene ilo linagwa kuchokera mu tharauza lake nkupita ku zala za nsapato zake. Mmodzi wa othandizira analipeza ilo, dzino loyikira lija. Ndipo Akazi a Graham anazinena izo pa iye, ali kuno. Ndipo chotero ine ndiri nalo ilo mchidutswa chaching'ono cha pepala, ine ndikuganiza kuti ndiri nalo ilo apa mu Baibulo langa.

¹⁵ Ndipo kotero izo ziri monga. . . pamene ife tiyamba kukalamba pang'ono ndi kubwanyuka, inu mukudziwa, ndi kuyamba kugwerula awa, zimapangitsa izo kukhala moipa. Ndipo chotero i. . . pamene ine ndinali uko ndi M'bale Roberson kumbuyo uko, ndi iwo, ine ndinali kuwatsuka iwo mmawa wina ndipo ndinaswa chidutswa pa iwo, ndipo ine ndinachita kuchitengera icho kwa adokotala, kuti akachikonze icho. Chotero Ambuye awonjezere madalitso Ake.

¹⁶ Tsopano ife tikuti, tsopano Ine ndikuti ndiyesere kudutswa mu lirilonse la iwo, ngati ine ndingathe. Ndipo, M'bale Tony, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndapeza tanthauzo la loto lanu, ndipo ilo linali lodabwitsa. Ndine wokondwa kwambiri kuti ndaliwona ilo. Ndipo ilo ndi tanthauzo labwino, limene ine ndikulingalira kuti ine sindikuyenera kulipereka ilo pagulu pano, kotero ine ndikupatsani inu ilo mwamseri ngati inu—ngati inu simuti. . . ngati inu mukufuna izo mwanjira imeneyo. Iye anandifunsa ine usiku wina, Iye anali ndi loto, ndipo ine sindimakhoza basi kumuuza iye chomwe ilo linali mpaka ine ndinapita kwa Ambuye ndi kukapempherera izo. Ndipo Ambuye anawululira ilo molibwezera kwa ine ndipo anandiiza ine chomwe kutanthauzira kwake kunali. Ndi zodabwitsa, ndi nkhani yabwino kwa inu, M'bale Tony.

¹⁷ Tsopano, mu funso loyamba. Tsopano, ine sindikudziwa basi kuti ndiyambire napo, chifukwa iwo onse ndi abwino. Koma, tsopano, ife tiyesera kuti tisakhale motalika kwambiri, ndipo mwinamwake ife tikhoza kudzawatsiriza iwo Lamlungu, ngati ife sitiwatsiriza iwo.

- 51. Fotokozani chomwe chimanthauza ndi “chilango chanthawizonse,” mu Mateyu 25:46. “Koma...” Ilo ndi funso.**
- 52. Ndiye, funso lachiwiri: “Koma ana aufumu adzaponyedwa ku mdima wakunja,” kodi izo ziri pafupi mofanana ndi kuwatayira iwo kunja kwa malingaliro a Mulungu?**

¹⁸ Chabwino, tsopano, kutenga funso lanu loyamba, lomwe likupezeka mu Mateyu Woyera, twente-... mutu wa 25. Tsopano ife ti... Tsopano, ine sindinawawerenge mowamvetsa konse awa, ndinangoyang'ana pa iwo kumbuyo uko, ndipo ndingoyesa mwakukhoza kwanga kuti ndiyang'ane pa iwo mwa kupambana komwe ine ndinga—momwe ine ndikudziwira kutero. Ndipo langa... Inu mutembenuze ndi ine mu Mabaibulo anu, pamene ife tikuwerenga kuti timvetse Ilo. Tsopano, ine ndimafuna kuti ndizitenge izi kuchokera mu Griki lexicon umunso, kuti inu mupeze—zapachiyambi zake. Ndipo i—ine ndimazikonda izo. Chotero ndiye ife tikhala nazo Izo monse—monse—Mchigriki ndi enawo. Ndipo tsopano izi zikhala—zikhala ngati zochedwerapo pang'ono, ndi kuwerenga kuti timvetse, chifukwa ine ndiyenera kuti ndifikire apo ndi kuwagwira Malemba basi paliponse pamene ine ndingawapeze iwo, ndi kuwatengera iwo pa malo awo. Chabwino.

¹⁹ Tsopano, alipo yemwe akufuna Baibulo kuti aziwerenga kuti amvetse nalo? Ngati inu mukutero, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndipo ife... ine ndikuganiza ife tiri nawo atatu kapena anai kumbuyo kuno. Ngati inu mukufuna kuti muwerenge kuti mumvetse ndi Lemba, chabwino. M'bale Cox, kodi inu mungabwere kuno ndi kudzanditengera ine Mabaibulo awa? Ndipo i—izo ndi zabwino kwa inu, ngati inu mungathe, kutero... (pali limodzi, ndipo inu basi—inu mungowatengera iwo pansu ngati inu mukufuna kutero, ochuluka choncho). Ndipo aliyense yemwe akufuna lina, ingonyamulani dzanja lanu, mnyamatayu awabweretsa iwo kwa inu komweko, mwaona. Ndipo ife tikufuna kuti tiwerenge kuti timvetse izi limodzi, ndi basi...

²⁰ Tsopano, pa kuwerenga uku ndipo mitu yotsiriza... mitu seveni yoyambirira ya Bukhu la Ahebri. Tikatha kuphunzitsa, ndithudi, mnyamata yemwe amazilemba izi, maphunziro awa, M'bale Mercier ndi M'bale Goad, ali nazo izo ndipo tsopano akukonzekera kuti azisindikize izo mwa bukhu. Ndipo iwo ali nazo izo. Tsopano... ndipo ife tiribe kanthu konga kungopesa mwa theka, ife tingokanda pamwamba. Ndipo ine ndikuganiza iwo amazitcha izo... ngati kutenga m—miyala yodula mu... ndi kungoipukuta miyalayo, miyala pang'ono yokha ya kuphunzitsa kwa Ahebri. M'bale Mercier akhala nazo izo posakhalitsapa, zitasindikizidwa, aliyense yemwe akuzifuna izo.

²¹ Tsopano izi mkati umu, izo zikubweretsa umu... Inu simungakhoze kupita modutsa... mu mpingo waulaliki, chomwe uno uli mpingo waulaliki. Inu simungakhoze kudutsa pa k—kuphunzitsa popanda kuutsa kukaikira ndi malingaliro a anthu ochuluka. Iwe umayenera kuteru. Tsopano, ine ndiri patali ndi kukhala mphunzitsi, sindine wolifotokoza Baibulo konse. Koma ine sindimayesera k—kuti ndinene chirichonse, kapena ngakhale kuti ndichite chirichonse, koma choyamba—poyamba ndimafunsa kapena ndimafufuza chinthu changa chopambana pa izo.

²² Izo zinafunsidwa kwa ine ndi m'bale wokonedwa, usiku watha, iye anati, “M'bale Branham, M'bale Seward nthawiina ananenapo kuti i—iwe sungakhoze basi kukupanikizani inu paliponse. Mwaona, kuti inu nthawizonse mumakhala ndi njira yina yozungulira yochokera mu izo kapena kuti muchoke kwa izo.”

²³ Ine ndinati, “Chabwino, chifukwa chake pa izo, ine nthawizonse ndimayesera kuganiza ine ndisanachite chirichonse. Mwaona? Ndiyeno ngati anthu andifunsa ine, ndiye ine ndikhoza kuwauza iwo chomwe maganizo anga anali. Mwaona?” Koma ziri ngati inu muganiza molondola. Ndipo inu musanachite chirichonse, ziyeserani kutenga mbali yomwe Mulungu akanafuna kuti inu mutenge, ndiye izo zikanakhaladi zovuta kuti wina akupanikizeni pena.

²⁴ Inu simukanalingalira nthawi yomwe—yomwe Ahabu ankayesera kumupanikiza Ahabu pansi. Kodi inu mukanakhoza kulingalira nthawi yomwe Afarisi ankayesera kumupanikiza Yesu pena? Mwaona, Iye anka—Iye ankayenera kuti ayankhe mofulumira, chifukwa chirichonse chomwe Iye ankachita, Iye ankachichita icho mwa chifuniro cha Mulungu, ndipo Iye... umo ndi momwe I—Iye ankakhoza kuzipezera izo. Tsopano, umo ndi momwe ife tikufunira nazo izi.

Tsopano funso lafunsidwa, ife tipitirira ndi funsola:

Tafotokozani chomwe zikutanthauza ndi “chilango chanthawizonse,” mu Mateyu 25:46.

²⁵ Tsopano mveterani mwatcheru kwenikweni. Aliyense tsopano, Mateyu 25:46:

Ndipo awa adzapita mu chiweruzo chanthawizonse: . . .

²⁶ Tsopano, funso ndilo, “Chiani. . . Tafotokozani. . .” Tsopano mawu oti *kwanthawizonse* amachokera ku mawu oti “*konse* ndi *nthawi zonse*,” ndipo *forever* ndi “danga la nthawi.” Izo zimangotanthauza “nthawi yochulukuka chomwechi,” monga *nthawizonse*. Tsopano ngati inu mutangowerenga... ine sindikudziwa yemwe analemba mafunsowo, chifukwa palibe

yemwe waika dzina lake pa iwo; izo sizimayenera kutero, ine sindikuwafuna iwo, mwaona.

Koma *awa adzapita ku chilango cha nthawizonse*: . . .
(tsopano penyani, awo ndi oyipa)

²⁷ Tsopano, wokonededwa—munthu wokonededwa yemwe wafunsa funsoli, ingowerengani zina zonse Zakezo:

. . . *koma olungama kumka ku moyo wamuyaya.*

²⁸ Oyipa adzapita ku chilango chanthawizosatha (kadanga kenakake ka nthawi), koma olungama ali ndi Moyo Wamuyaya. Inu simudzapeza konse chilango Chamuyaya, sicingakhoze kukhala chiri. Mwaona, ngati iwo ali ndi chilango Chamuyaya, iwo ali ndi Moyo Wamuyaya; iwo akakhala ndi Moyo Wamuyaya, iwo ndi opulumutsidwa. Onani, izo sizingakhoze kukhala ziri. Tsopano ngati inu muti mupenye, f—funsolo ladzifunsa lokha . . . likudziyankha lokha. Mwaona?

Ndipo awa . . .

Tsopano penyani, ine ndatenga tisanafike apa:

. . . *ndipo iwo* . . .

²⁹ Mu wa 20 . . . ndime ya 44:

. . . *ndipo iwo nawonso anayankha, nati kwa Iye, Ambuye, ndi liti pomwe* ife sitinakhale ndi *njala*, ndi liti tinakhala ndi ludzu, ndi *mlendo*, ndi *wamaliseche*, . . . ndi *mu ndende, ndipo sitinatumikire kwa inu?*

Ndiye i—ndiye iye adzawayankha iwo, kuti, Indetu ine ndikuti kwa inu, Mochuluka monga inu munachita izo . . . kwa mmodzi wa aang'ono awa, inu munazichita izo . . . kwa ine.

Ndipo awa adzapita ku chanthawizonse (everlasting) *chilango*: (awo ndi oyipa) . . . *koma olungama ku Moyo Wamuyaya.*

³⁰ Mukuona kusiyana kwake? Oyipa ali ndi chilango chanthawizonse, koma *everlasting* ndi “kadanga ka nthawi.” Tsopano, ngati izo zikanakhala zofanana, izo zikanalembedwa, “Ndipo awa adzapita ku chilango chanthawizonse, enawo adzapita ku moyo wanthawizonse.” Mwaona? Kapena, “Iwo adzapita ku chilango Chamuyaya, ndipo enawo adzapita ku moyo Wamuyaya.” Mukuona, ngati kuli chilango Chamuyaya, kuti akalangidwe kwanthawi za nthawi, ndiye kuli Muiyaya . . . iye ali nawo Moyo Wamuyaya; ndipo Moyo Wamuyaya umodzi wokha, ndipo iwo umabwera kuchokera kwa Mulungu. Chirichonse chopanda chiyambi chiribe mathero, chirichonse chiri ndi chiyambi chiri ndi mathero. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

³¹ Tsopano, Lemba Palokha lomwe—munthu wokonededwayu wayankha . . . Tsopano ngati inu mungazitengere izo mu lexicon,

“*Ndipo awa adzapita ku ainion, kudulidwa nachotsedwa, ndi ku nthawi... ndi ku moto, nyanja ya moto.*” Tsopano, mawu oti a-i-n-i-o-n amatanthauza “danga la chilango.” Mu lexicon ya Chigriki, pomwe pano, “danga la chilango,” kapena, “nthawi ya chilango.” Mwaona, “Iwo adzapita mu nthawi ya chilango.” Mawu omwe akugwiritsidwa ntchito, a-i-n-i-o-n. Ainion, omwe akutanthauza “nthawi, nthawi, nthawi yoikidwapo.” Ndiye muzitengere izo mmbuyo mu—mu kumasulira apa, Chingerezi, *nthawizosatha* ndi “nthawi yoikidwapo.” Mwaona, iwo akubwera kuchokera ku Chigriki, “nthawi yoikidwapo.” Mawu oti *ainion*, kapena *a-i-n-i-o-n*, *ainion* amatanthauza “nthawi yoikidwapo ya chilango.”

³² Komano muwerenge enawo, “Koma awa adzapita ku Muyaya.” Uko ndi kusiyana kwake. Mwaona, Moyo Wamuyaya. *Umuyaya* umabwera kuchokera ku mawu a “Muyaya,” ndipo Umuyaya unalibe chiyambi ngakhale mapeto. Ndi kwanthawi *ndi* nthawi. Tsopano izo ziyenera kuyankha zija, mwaona, chifukwa ngati inu mutati mungowerenga Lemba mwatcheru kwenikweni, inu muwona.

³³ “*Ndipo awa adzapita ku chilango chanthawizosatha, koma olungama...*” Oipa adzapita ku chilango chanthawizosatha, kukalangidwa kwa danga la nthawi; mwinamwake mu zaka bilioni, ine sindikudziwa, koma inu zedi inu mudzakalangiwa chifukwa cha machimo anu. Koma zedi monga tchimo linali ndi chiyambi, tchimo liri nawo mapeto. Chilango chinali ndi chiyambi, ndipo chilango chiri ndi mapeto. Ndipo gehena analengedwera kwa Mdierekezi ndi angelo ake. Mwaona? Chabwino. Tsopano, ine ndiri nalo lina pansu apa loti ndiyankhire mu izo, mu maminiti pang’ono okha, lomwe liri lokongola, lomangirizira mu ilo.

Tsopano, koma awa apa: “**Koma ana aufumu adzaponyedwa kunja mu mdima,**” kodi izo ziri pafupi zofanana ndi kuwaponyera iwo kunja kwa malingaliro a Mulungu?

³⁴ Ayi, izo sizikanakhala ziri zofanana. Tsopano, inu mukulozera apa ku Mgonero wa Chikwati. Tsopano, “Ndipo ana aufumu,” monga zinafunsidwira apa. Ana aufumu ndiwo Ayuda, ndipo iwo anaponyedwera kunja kwa mdima. Ndipo i—iwo akhala ataponyedwa ku mdima wakunja, ndipo iwo adutsa mu nthawi ya kulira ndi kusisima ndi kukukuta kwa mano. Iwo anaponyedwa ku mdima wakunja chifukwa izo zikanakupatsani inu ndi ine danga loti tilape, koma iwo sanaponyedwere konse kunja kwa malingaliro a Mulungu. Iye sadzamuiwala konse Israeli. Ndipo Israeli, monga wowerenga Baibulo aliyense amadziwa, iwo amanenedwa ngati “ana a ufumu.” Mwaona, ndi ufumu, lonjezo. Mwa kuyankhula kwina, Mulungu kuchita ndi fuko, pamene Iye ankachita ndi Israeli, omwe ali ana a ufumu.

³⁵ Tsopano, inu kumbukirani, Iye anati apo, “Ndipo Abrahamu ndi Isaki ndi Yakobo,” mu malo amodzi, “akanadzabwera ndi kudzakhala mu ufumu pa nthawi yotsiriza.” Mwaona, ndipo kuti Abrahamu, Isaki ndi Yakobo akanadzakhala ali mu ufumuwo; iwo anali, iwo anali anthu odalitsidwa a ufumu. Koma ana a ufumu adzaponyedwa ku mdima wakunja.

³⁶ Tsopano, pamene zonedwazi zikuchokera apa ndi pa—ndi Mkwati. Pamene Mkwati akudza, pamene iwo anali... Asanu a anamwali anapita kuti akakomane ndi Ambuye, n—ndipo iwo sanatenge mafuta aliwonse mu nyali yawo. Ndipo e—ena asanuwo anatenga mafuta mu nyali zawo. Tsopano, ngati inu mungazindikire, ndi chithunzi chokongola, onse Myuda ndi Amitundu, ngati okanidwa. Musunge mu malingaliro kuti pali mitundu itatu ya anthu nthawi zonse: Myuda, Wamitundu (wachizolowezi),...; Myuda, Wamitundu, ndi Mpingo. Ngati inu mutenga izo mosakaniza, inu ndithudi mulowa mu vuto pamene inu muti mugunde Chivumbulutso. Pakuti ngati inu simutero...

³⁷ Monga Bambo Bohanon anati kwa ine nthawi yina, anati, “Billy, aliyense yemwe angayesere kuti awerenge Chivumbulutso angakhale ndi malubwelubwe. Bwanji,” iye anati, “apa pali Mkwatibwi pansi apa pa dziko lapansi, n—ndi chinjoka chikulavula madzi kuchokera nkamwa mwake kuti chipange nkondo naye.” Ndipo anati, “Ndiye nthawi yomweyo kuti Mkwatibwi akuima ngati handiredi forte foro sauzande” (chiphunzitso cha Mboni za Yehova) “pa Phiri la Sinai. Ndipo pa nthawi yomweyo Mkwatibwi ali Kumwamba.” Ayi, ayi, inu mukulakwitsa.

³⁸ Pali mitundu itatu ya anthu. Mukuona, awo ndi, Myuda wokanidwa, ndipo apo palinso namwali wogona yemwe madzi... Iyo si Mbewu ya mkazi, ndi otsalira a Mbewu ya mkazi omwe chinjoka chinali kulavula madzi kuchokera nkamwa mwake... Chivumbulutso 11. Ndiyeno, makamaka, Ayuda handiredi ndi forte foro sauzande anali mwamtheradi osati Mkwatibwi, iwo ndi otsalira a mpingo wa Chiyuda. Ndi chiphunzitso cha Mboni za Yehova chimene chimawaika iwo ngati Mkwatibwi, ine sindikuwona momwe inu mungakhoze kuchitira izo, chifukwa, uyo si Mkwatibwi.

³⁹ Ngati inu mungazindikire uko mu Chivumbulutso umo, Ilo likuti, “Ndipo iwo ndi anamwali, Ndipo iwo ndi adindo.” Ndipo kodi mdindo anali chiani? Iwo anali... Mdindo anali olondera pa kachisi omwe ankailondera mfumukazi, chifukwa iwo anali... ch-... Iwo anali amuna omwe anapangidwa kukhala osabala. Iwo anali... Kodi inu munazindikira, anati, “Iwo anali asanadziipitse okha ndi akazi”? Iwo anali adindo a mkachisi. Ndipo iwo anali chiwerengero chosankhidwa chomwe Mulungu anali atachitenga kuchokera mwa osankhidwa a Chiyuda. Tsopano, ngati inu mungazindikire... Ngati ife

tingati tingozitenga izo mphindi yokha, kuti tikhale ngati tazikhazikitsa izo mu malingaliro anu, pamene inu mungakhoze kwenikweni. . .

⁴⁰ Tiyeni titenge Chivumbulutso, mutu wa 7, ndipo ife tipeza apa tsopano, pamene. . .chomwe Ilo linanena. Ndi chinthu chokongola:

Ndipo zitachitika izi. . .ine ndinawona angelo anai ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi, . . . (tsopano, izi zikuyendera limodzi ndi Ezekieli 9, pamene iye anawona chiwonongeko cha Ayuda. Ndipo apa iye akuwona chiwonongeko cha Amitundu, Chivumbulutso, mutu wa 7) . . .Ndipo ine ndinawona angelo anai ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi, atagwirizira mphepo zinai (mphepo zimatanzauza “nkhondo ndi makangano”) . . .kuti mphepo isawombe pa dziko, ngakhale pa nyanja, . . .kapena mtengo uliwonse. (ndipo iyo ndi nkhondo, “kugwirizira”)

⁴¹ O, ngati ife tikanakhala nayo nthawi yoti tipite mwa dongosolo pa funso ili. Izo zinachitika. . .Apo ndi pamene Russell anasokonezekapo. Russell ananenera, powona izi zikudza. Iye ananenera “uko kukanakhala kuli kudza kwa Ambuye Yesu,” asali kudziwa kuti uko kunali—kusindikizidwa kwa Mpingo. Mwaona?

⁴² Ndipo iwo anadabwa momwe nkhondo ya dziko. . . Nkhondo Yoyamba Yamdziko lonse. Onani, iyo inatha pa Novembala leveni, pa leveni koloko masana; mwezi wa leveni, tsiku la leveni, ndi ora la leveni. Ndipo mwamsanga zitachitika izo, ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu unawululidwa ndi Ubatizo wa Mzimu Woyera kwa Mpingo. Ndendende, mwamsanga zitachitika izo.

⁴³ Ngati inu mutazitengera izo uko ku Chivumbulutso, momwe ife tinazimangira Izo limodzi, ndipo pakati pa M’badwo wa Filafelfia ndi wa Laodikaya. Ndipo Achimethodisti anali ndi M’badwo wa Chifiladelfia, chikondi cha mwaubale. Ndipo m’badwo wotsiriza, m’badwo wa mpingo, unali M’badwo wa Chilaodikaya, umene unali m’badwo wofunda. Ndipo Iye anati mmenemo, “Ine ndaika khomo (khomo lotseguka) patsogolo panu.” Khomo lotseguka! Ndipo ngati inu mungafufuzire Malemba amenewo mmbuyo, iwo amangiriza Uthenga wonsewo mpaka mu malo amodzi awo apo, kuti akusonyezeni inu izo ndendende.

⁴⁴ Penyani! Apa kuti chirichonse chinali chiri Atate, Mwana, Mzimu Woyera, mu ubatizo, (chomwe ife titi tifike mu izo molunjika) zomwe zinali mwamtheradi chikhulupiriro cha Chikatolika ndipo osati konse chiphunzitso cha Chikhristu. Ayi, bwana. Ine basi. . .Ife tiri nazo izo pomwe pano, usikuuno, kuti tifike mu izo; ndi lexicon, aponso. Mwaona? Inde, bwana, ndi mbiriyakale nayonso. Panalibe aliyense anayamba

wabatizidwapo monga choncho mu Baibulo, kapena osati kwa zaka sikisi handiredi zoyambirirazo litakhalapo Baibulo. Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira izo pomwe pano mwa chiphunzitso cha Chikatolika chawo chomwe, kuti iwo ndi omwe anaziymbitsa izo, ndi kukonkha ndi kutsanulira.

⁴⁵ Izo zinabwera kuchokera kumeneko kupita mu mpingo wa Chiwesile, ndi mpaka ku mpingo wa Chimethodisti, Achimethodisti anachibweretsa icho mpaka kwa Abaptisti, Abaptisti anachibweretsa icho mopitiriza, ndipo icho chikadali chiphunzitso chabodza! Ndipo tikhoza kubwerera mu Baibulo ndi kutsimikizira kwa inu kuti Baibulo linanena kuti “inu muli nalo dzina loti ndinu amoyo, koma ndinu okufa.” Ndizo ndendende kulondola. Ndipo iwo anali . . .

⁴⁶ Ine ndikhoza kutsimikizira kuti Baibulo linaphunzitsa kuti iwo akanati azigwiritsa ntchito Dzina Lake mu ubatizo mpaka mu m’badwo wa mdima, malingana ndi—m’badwo wachinai . . . wa—m’badwo wa mpingo, m’badwo wa mpingo wa Pergamo. Ndipo Iye anati, mu, zaka fiftini handiredi za mibadwo ya mdima izo, aliyense, ankati, “Inu muli nako kuwala pang’ono kwatsalira, chifukwa inu simunalikane Dzina Langa.”

⁴⁷ Pamene izo zinafika ku m’badwo wina uja uko, m’badwo wa Chikatolika, Iye anati, “Inu muli nalo dzina loti inu ‘muli moyo,’ koma ndinu okufa! Ndipo inu mwalikana Dzina Langa.” Ndi inu apo. Mwaona? Izo zonse zikungomangiriza chithunzi chimodzi chokongola chachikulu limodzi, Baibulo lonse.

⁴⁸ Tsopano zindikirani izi:

. . . *kuwirizira mphepo zinai . . .*

Ndipo ine ndinamuwona mngelo wina akutsika kuchokera Kumwamba, ali ndi chisindikizo cha Mulungu wamoyo: . . . (chisindikizo)

⁴⁹ Tsopano, kodi chisindikizo cha Mulungu wamoyo ndi chiani? Tsopano, inu abale a Advent mufuna munene kuti, “Kusunga tsiku lasabata.” Ine ndikufuna kuti inu mundisonyeze ine izo mu Lemba. Izo siziri mmenemo. Palibe malo amodzi anachita izo . . . c—chiri chisindikizo . . .

⁵⁰ Ngati inu mutawerenga Aefeso 4:30, mofulumira ndithu, inu mupeza chomwe Chisindikizo cha Mulungu wamoyo chiri. Aefeso 4:30 amati, “Musaukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Osati mpaka chitsitsimutso chotsatira, koma muli ndi chitetezero chamuyaya (unhu). “Musaukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu womwe inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Onani ngati Aefeso 4:30 samanena zimenezo, ndiye mutenge zowerenga zanu za mmalire ndi kuziyendetsa izo njira yonse kudutsa mu Malembawo mmenemo, ndi kupezamo. Tsopano, “Osindikizidwa mpaka

tsiku la chiwombolo chanu. Muli ndi chisindikizo cha Mulungu wamoyo.”

51 Tsopano, kumbukirani, Mzimu Woyera sunali kuphunzitsidwa ngati Ubatizo wa Mzimu Woyera mpaka itatha Nkhondo ya Dziko lonse Yoyamba. Iye tangokondwerera kumene c—chikondwerero chathu chagolide, zaka forte, kapena chaka cha forte cha chisangalalo.

. . . ndipo iye anafuula ndi mawu aakulu kwa angelo anai, omwe anapatsidwa kuti aliwononge dziko lapansi kapena nyanja,

Kuti, Musaliwononge dziko lapansi, ngakhale nyanja, kapena mtengo uliwonse, mpaka ife titawasindikiza antchito. . . (tsopano inu mukufika ku funso lanulo, “ana,” mwaona). . . antchito a Mulungu wathu mu mphumi zawo. (musapweteke, musaliwononge dziko lapansi, musati mulole bomba la atomiki kuti liphulitsidwe, musati mukhale ndi chinthu chathunthu mpaka antchito a Mulungu wathu atasindikizidwa)

52 Tsopano, ngati ife tingakhoze kuzitengera izo mmbuyo patali ndi kupita nazo mmbuyo umo, momwe k—kuti ngakhale pa *Kutha kwa Nkhondo ya mDziko lonse*, mu mpukutu wachiwiri, pamene Mkulu Wankhondo Allenby anamenya mpaka iye anagunda mizere ya ku Yerusalemu, ndipo iye basi anatumizanso lamya kwa Mfumu yaku England, ndipo anati, “ine sindikufuna kuti ndiwombere pa mzindawo, chifukwa cha kutapulika kwa iwo.” Iye anati, “Kodi ine ndichite chiani?”

53 Iye anati, “Pemphera.”

54 Ndipo iye anawulukira pamwamba pakeponso, ndipo pamene iwo anatero, iwo anati, “Allenby akubwera.” Ndipo munali Achimuhamadi mkati umo, anaganiza kuti iye ankati, “Allah akubwera.” Ndipo iwo anakweza mbendera yoyera nadzipereka ndipo Allenby anaguba nalowa mu Yerusalemu ndipo anaulanda iwo popanda kuwombela chipolopolo, molingana ndi mauneneri. Ndiko kulondola, ndipo anauperekanso iwo kwa Ayuda.

55 Ndiye iwo anautsapo Hitler kuti akawazunze Ayuda, ndipo konsekonse mdziko, ndipo anawathamangitsa iwo kubwerera uko.

56 Ndipo Baibulo linati Iye akanati “adzawabweretsenso iwo pa mapiko a mphungu.” Ndipo pamene iwo ayamba kubwerera. . . *Life Magazine* ndi zinazo zinalembe izo mu masabata angapo apitawo, kumene iwo anawabweretsanso iwo mu zikwi, kukalowa mu Yerusalemu, ndipo iwo anapita nakawanyamula okalamba awo pa misana yawo. Iwo anafunsidwa. Ine ndiri nazo izo pa kanema ndi chithunzi. Ndipo iye anati. . . Apo panali mbendera ya nyenyezi yambali zinai

ya Davide, itapachikidwa apo; mbendera yakale kwambiri mu dziko, nthawi yoyamba yomwe iyo inaulutsidwa kwa zaka thuu sauzande.

⁵⁷ Yesu anati, “Pamene mtengo wa mkuyu uyamba kuonetsa mphukira zake, m’badwo uno sudzatha.”

⁵⁸ Ndipo apa iwo anali akuwabweretsa okalamba awo, ndipo anati, “Bwanji? Kodi inu mukubwerera kuti mudzafere mdziko lakwanu?”

⁵⁹ Anati, “Ayi, ife tabwera kuti tidzamuwone Mesiya.”

⁶⁰ Ndipo, m’bale, ine ndikukuuzani inu, ife tiri pa khomo! Ndi awo antchitowo, omwe akudikirira kumusi uko. Osati gulu ili la Ayuda lomwe lingakunamizeni inu ndi mano anu oyikirira ngati iwo angathe, uyo si Myuda yemwe Iye akumukamba. Koma ndi awo kutali uko omwe asunga—malamulo ndi zinthu, ndipo samadziwa nkomwe ngakhale kuti kunali Mesiya.

⁶¹ Ndipo M’bale...ku Stockholm, M’bale Petrus, anawatumizira iwo uko Zipangano Zatsopano milioni, ndipo pamene iwo anazilandira izo akuziwerenga izo. Iwo anati, “Chabwino, ngati uyu ali Mesiya, tiyeni ife timuwone iye akuchita chizindikiro cha mneneri, ndipo ife timukhulupirira iye.”

⁶² Khwekhwe lakelo kwa utumiki wanga! Ine ndinali pafupi maora awiri ndi zipata zaku Yerusalemu, kuti ndipite mmenemo, ndipo ine ndinali ku Cairo, Egypt. Ndipo ine ndinali ndikuyenda kumeneko, ndipo Mzimu Woyera unati, “Usati upite tsopano.”

⁶³ Ine ndinaganiza, “Ine ndimangolingalira izo. Tikiti yanga yagulidwa kale, ine ndiri paulendo wanga. Munthu ali uko woti akakomane nane, gulu lonse, masukulu ndi ena otero.”

⁶⁴ Ine ndinayenda patsogolo pang’ono, ndipo Mzimu unati, “Usati upite! Usati iwe upite.”

⁶⁵ Ine ndinabwerera kwa wogulitsa matikiti, ine ndinati, “Ine ndikusintha tikiti iyi. Ine ndikufuna kuti ndipite ku Athens, Greece, ku Phiri la Mars.”

⁶⁶ Ndipo iye anati, “Chabwino, kopita kwa tikiti yanu ndi ku Yerusalemu, bwana.”

⁶⁷ Ine ndinati, “Ine ndikufuna kuti ndipite ku Athens mmalo mopita ku Yerusalemu.” Mzimu Woyera ukudikira, ora limenelo silinabwere panobe. Izo siziri moyenera basi.

⁶⁸ Penyani:

...anasindikiza antchito a Mulungu wathu mu mphumi zawo,

Kumati, Musati muliwononge dziko lapansi,... mpaka ife...titawasindikiza antchito a Mulungu wathu mu mphumi zawo. (aliyense akudziwa kuti icho ndi Chisindikizo cha Mzimu Woyera; penyani)

Ndipo ine ndinamva chiwerengero cha iwo omwe anasindikizidwa: . . . (tsopano, ngati awo si Ayuda, penyani ichi) . . . ndipo apo anasindikizidwa handiredi n forte-oro sauzande onse a mafuko a ana a Israeli. (mulibe Amitundu mkati mwawo. Apo ndi pa nthawi yotsiriza)

⁶⁹ Penyani! Fuko la Yuda, thwelofu sauzande; fuko la Rubeni, thwelofu sauzande; ndi mpaka mmusi, Gadi, thwelofu sauzande; Nefitali, n—n—ndi njira yonse mpaka kwa Aseri, ndi—Zabuloni, ndi mafuko onse thwelofu awa a Israeli. Ndipo thwelofu kuchulukitsa ka thwelofu ndi chiani? Handiredi n forte-oro sauzande. Ndi awo handiredi n forte-oro sauzande, Ayuda! Osati Amitundu, Ayuda! Icho si chinthu chochita ndi Mkwatibwi. Kotero Mboni za Yehova ziri kulakwitsa pa chiphunzitso chawo. Baibulo limanena mwachimvekere kuti awo ndi “Ayuda,” ndipo osati Amitundu. Iwo ndi antchito a Mulungu, ndipo Amitundu sankatengedwa konse ngati antchito. Ife ndi ana aamuna ndi aakazi, osati antchito.

⁷⁰ Tsopano werengani zonse za Iwo. Monga munthu akudya vembe, anati, “Iyo njabwino, koma tipatseniko zochulukira za iyo.” Chabwino, Mulungu ali nazo zochuluka za Izo pano. Tsopano, tangozindikirani. Tsopano, tsopano ife tiri pa ndime ya 8:

Ndipo a fuko la Zabuloni . . . anasindikizidwa thwelofu sauzande. Fuko lonse la Yosefe anasindikizidwa thwelofu sauzande. A fuko la Benjamini anasindikizidwa thwelofu sauzande.

⁷¹ Mwaona, Yohane, pokhala Myuda, anamuzindikira aliyense wa iwo, anawaona mafuko khumi ndi awiri a Israeli; thwelofu sauzande kuchokera mu fuko lirilonse, thwelofu kuchulukitsa ka thwelofu kukhala handired n forte-oro sauzande. Ndi awo apo, osati Mpingo, Ayuda. Baibulo linanena apa, iwo anali onse “ana a Israeli,” fuko lirilonse linatchulidwa.

⁷² Tsopano penyani, ndime ya 9:

Zitachitika izi (tsopano apa pakudza Mkwatibwi) . . .

Zitachitika izi ine ndinawona, . . . taonani, gulu lalikulu, limene palibe munthu akanakhoza kuliwerenga, . . .

⁷³ Uyo ndi mdindo wanu wa mkachisi, iwo ali basi handiredi n forte-oro sauzande, kamalo kakang’ono basi, olondera kachisi pang’ono awa omwe ati azidzakhala ali ndi Mkwatibwi; basi Ake—omperekeza Ake basi. Ndiwo handiredi n forte-oro sauzande, ndi operekeza kwa Mkwatibwi; adindo a mkachisi.

⁷⁴ Penyani! Ndithudi, ine ndikudziwa kuti inu mubwerera uko mpaka ku ya 14, nkuti, “Chifukwa chiani, iwo akukhala ndi Mkwatibwi kulikonse komwe iwo. . .” Mwamtheradi! Adindo

ankayenda ndi mfumukazi kulikonse komwe iye ankapita. Moonadi! Koma kodi iwo anali chiani? Iwo sanali kanthu koma operekeza, ndipo ndizo ndendende zomwe Lemba likulongosola kuti ali apa.

75 Zindikirani:

Ndipo zitachitika izi...ndipo, taonani, gulu lalikulu, limene palibe munthu akanakhoza kuliwerenga, la mafuko onse,...mitundu,...anthu, ndi lirime,... (ndi uyo Mkwatibwi wanu wa Amitundu akudzapo, chabwino)...awa anaima... pamaso pa Mwanawankhosa, (ndi uyo Mpulumutsi wawo, Mwanawankhosa, osati lamulo; Mwanawankhosa, Chisomo)...atavekedwa ndi miinjiro yoyera,... (penyani, mu maminiti pang'ono, muwone ngati miinjiro yoyera siili chilungamo cha oyera)...ndi kanjedza mu dzanja lawo;

Ndipo iwo anafuula ndi liwu lopokosera,... (ngati ichi si chitsitsimutso cha chipentekoste, ine sindinayambe ndamvapo china)...kumati, Chipulumutso kwa Mulungu wathu yemwe wakhala pa mpandowachifumu, ndi kwa Mwanawankhosa.

Ndipo angelo onse anaima kuzungulira pa mpandowachifumu, ndi pafupi ndi akulu ndipo zamoyo zinai,...zinagwa pa...pamaso pa mpandowachifumu pa nkhope zawo, ndipo zinampembedza Mulungu,

Kumati, Amen: Madalitso,...ulemerero,... nzeru,...mathokozo,...ulemu,...nyonga, mphamvu, zikhale kwa Mulungu wathu kwanthawi za nthawi. Amen.

76 Izo zikumveka ngati nthawi ya msonkhano wa msasa, si choncho? Zikhala ziri! Anali ndani awo? Handiredi n forte foro sauzande? Osati nkomwe! Chiwerengero chachikulu ichi chimene palibe munthu...a mitundu yonse, malirime, ndi mafuko. Kodi inu simungakhoze kuwona, mzanga wokonedwa?

77 Tsopano penyani, tingowerenga Izo. Tsopano:

Ndipo mmodzi wa akulu anayankha, nati kwa ine, Kodi awa ndi ndani ndi...omwe avala miinjiro yoyera? Ndipo kodi iwo akuchokera kuti?

78 Mkuluyo anati kwa Yohane, yemwe anali Myuda yemwe anawazindikira handiredi n forte foro sauzande'wo, anati, "Tsopano, iwe unawadziwa awo, iwo onse ndi Ayuda. Koma kodi awa ndi ndani? Kodi iwowo achokera kuti?" Mukuona chimene mkuluyo ananena? "Mmodzi wa akulu anayankha," (awo ndi akulu a ku Mpandowachifumu) "anandiyankha ine, nati, 'Kodi awa ndi ndani omwe avala miinjiro yoyera? Ndipo

kodi iwo achokera kuti? Tsopano, ife tonse tikuwadziwa Ayuda ndi pangano lawo ndi zina zotero, koma kodi awa anabwera liti?” Tsopano penyani:

Ndipo ine ndinanena kwa iye, Bwana, ndinu mukudziwa. (“I—i—ine sindiri,” Yohane anati, “izo basi zandidutsa ine. Ine sindikudziwa.”) Ndipo iye anati kwa ine, Awa ndi iwo omwe anabwera kuchokera mu zisautso zazikulu, (“Kupyola mmayesero ndi zowopsya zambiri izi, zovutikira ndi misampha, ine ndadzeramo kale.” Mwaona?)...awa akubwera kuchokera mu zisautso zazikulu, ndipo atsuka mwinjiro wawo,... (mu mpingo? Kodi izo zikumveka molondola?)... atsuka miinjiro yawo, ndipo ayiyeretsa iyo mu magazi a Mwanawankhosa.

...iwo ali ku mpandowachifumu wa Mulungu, ndipo akumutumikira Iye usana ndi usiku... (ndani amanditumikira ine mu nyumba yanga? Mkazi wanga. Ndi kulondola uko?)...ndi mu kachisi Wake:... (ndi yemwe amakhala ndi ine mnyumba yanga ndi mu chuma changa, ndi mkazi wanga. Iye ndi yemwe amakhala ndi ine, ndipo amachapa zovala zanga, ndi kukhala atandikonzera kale zinthu ine)...ndipo iye amene wakhala pa mpandowachifumu azikhala pakati pa iwo. (O, mai, mvetserani!)

Ndipo iwo sazimva njala kenanso,... (zikuwoneka ngati iwo anali ataphonya zakudya kangapo pobwera uko)...ngakhalenso iwo sadzamva ludzu kenanso; kapena dzuwa kuwalira pa iwo kenanso, ngakhale kutentha kulikonse.

Pakuti Mwanawankhosa yemwe ali pakati pa mpandowachifumu azidzawadyetsa iwo, ndipo azidzawatsogolera iwo kupita ku kasupe wa madzi amoyo: ndipo Mulungu adzapukuta...misozi yonse kuichotsa pa maso awo. (ndi Uyo apo, ndi uyo Mkwatibwi wanu)

⁷⁹ Apo pali handiredi n forte foro sauzande anu, ndipo apo pali antchito anu. Kotero “ana a Ufumu” apa, munthu wokonedwa yemwe anafunsa funsoli, ndi...yemwe anafunsa funso lodziwika ili. Ine ndikuganiza ine mwina ndinazisiyira izo mmbuyo umu mu...penapake, koma “pamene iwo ati adzaponyedwe kunja,” izo sizikutanthauza kuti iwo adzaponyedwa kuchoka mu malingaliro a Mulungu. Iwo akuponyedwera kunja kwa phindu lauzimu kwa nyengo. Mwaona, kwa kanthawi kakang’ono kokha.

⁸⁰ Chifukwa, pamene mneneri anamuwona Israeli mu tsiku ili kuti iye anali kubwerako, iye anati, “Chabwino, kodi Israeli adzakhalapo pamene Sabata liti lizidzachotsedwa, n—ndipo

iwo akumagulitsa pa Sabata chimodzimodzi monga tsiku lina lirilonse, ndi zinthu zonse izi.” Iye anati, “Chabwino, kodi Inu—kodi Inu mudza . . . Kodi Israeli adzaiwalidwa kwathunthu?”

⁸¹ Iye anati, “Kodi kumwamba nkutali chotani? Ndi pokuya bwanji pansipa? Yeza izo ndi ndodo ili patsogolo pakoyo.”

Iye anati, “Ine sindingakhoze!”

⁸² Iye anati, “Ngakhalenso ine sindingathe konse kumuiwala Israeli.” Ndithudi ayi! Israeli sadzaiwalidwa konse.

⁸³ Kotero inu mukuona, *nthawi zonse* ndi *Muyaya* ndi zinthu ziwiri zosiyana. Israeli anatayidwa kunja, koma osati kunja kwa malingaliro a Mulungu. Ndipo Paulo akuziyankhula izo kuno, ngati ine ndikanakhala . . . ndikanakhala nayo nthawi yoti ndiziwerege, kuti ine ndikhoze kufika mofulumira ku Lemba lomwe . . . Ine ndikanakhoza kulozera izo kwa inu, mwaona, izo zikubwera mu malingaliro anga.

⁸⁴ Paulo poyankhula pamenepo, ananena izo kuti ife Amitundu tisamalitse, momwe ife tiyendera ndi zomwe tichita. Mwaona? Chifukwa ngati Mulungu sanailekerere nthambi yoyambayo, mwaona, ndipo ife pokhala ongomezanitsidwa umo, mwaona, . . . Ndipo Israeli, yemwe anachititsidwa khungu kwa kanthawi, iye anati. Kwa kanthawi kokha, Israeli anachititsidwa khungu. Uko nkulondola, koma chophimbacho chidzachotsedwa pa maso awo. Ndipo apo ndi pamene Wamitundu wotsiriza adzabadwira mu Ufumu wa Mulungu, ndiye chophimba chawo chikuchotsedwa pa maso a Israeli. Ndipo iwo adzati, “Uyu ndi Mesiya yemwe ife tinkamuyembekezera kuti timuwone.” Uko nkulondola, koma khomo la Amitundu latsekedwa (likasa—latsekedwa), palibenso—palibenso chisomo chidzatsalira kwa Amitundu pa nthawi imeneyo.

⁸⁵ Tsopano, ine ndatenga nthawi yonse yochulukika pa funso limodzi. Ndipo winawake ati, “Tsopano inu simukufika ku langa.” Chabwino, ife tifulumirapo ndi kuwona ngati ife sitingakhoze kufika kwa ilo.

⁸⁶ Chabwino, apa pali—limodzi lalitali. Ndipo chidutswa chirichonse cha zomwe mkazi anafunsa kapena bamboyo amafunsa, kapena aliyense yemwe ali, ndi zolondola.

53. Kodi si zoonza kuti Ambuye Yesu sanafere dziko lapansi lonse, kutanthauza aliyense mu dziko, koma maka . . . (tsopano, ine ndingafotokoze izo, koma iye . . . mwamuna kapena mkazi, aliyense yemwe ali . . . Zikuwoneka ngati zolemba za mkazi) . . . **koma maka kwa awa—maka kwa awa ali mu zigawo zonse za dziko lapansi, omwe Atate anamupatsa Iye? Awa omwe asanaikidwe maziko a dziko, Mulungu anali atawadzozeratu ku Moyo Wamuyaya, atawasankha iwo molingana ndi kukondweretsedwa Kwake komwe kwabwino?**

⁸⁷ Mwamtheradi, uko nkulondola! Ndizo ndendende kulondola. Yesu anafera . . . osati kungoti . . . Iye ankalinga.

⁸⁸ Tiyeni tiwone, ine ndikukhulupirira . . . I—ine ndikukhulupirira iwo anawerenga . . . funso likubwerapo pa izi:

54. Lemba mosakaika limatiuza ife kuti awa ndi iwo omwe sadzati. . . ndi iwo omwe sati adzapulumutsidwe. Chotero. . .

⁸⁹ Ndizo ndendende kulondola. Lemba limatiuza ife kuti alipo anthu omwe anadzozedweratu ndi Mulungu kuti adzaweruzidwe.

⁹⁰ Kodi inu mungafune kuti muwerenge izo, kotero izo nthawizonse zizikhala ziri kunja kwa malingaliro anu? Chabwino, tiyeni titembuzire uko tsopano ku Bukhu I—la Yuda, Yuda akuyankhula apa.

Yuda, wantchito wa Yesu Khristu, m'bale wa Yakobo, kwa iwo omwe ali oyeretsedwa ndi Mulungu Atate, ndipo atasungidwa mwa Yesu Khristu, ndipo ataitanidwa:

⁹¹ Mukuona omwe Iye akuwalemba Iyo? Osati kwa wochimwa, osati msonkhano waulaliki chabe, koma kwa oyeretsedwa ndi oitanidwa. Mukuona, iwo omwe ali kale mu Ufumu.

Chifundo kwa inu, ndi mtendere, ndi chikondi, zichulukitsidwe.

Okonedwa, . . . ine ndikupereka kulimbika konse kuti ndikulembere ni inu za chipulumutso wamba, chinali chofunikira kuti ine ndikulembere ni inu, ndi kukulimbikitsani inu. . . muyenera inu moonamtima muzilimbikira chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera.

Pakuti pali anthu ena akwawiramo mosadziwika, omwe anali kale atadzozedwera ku chiweruzo ichi, . . . (motani?) . . . kusandutsa chisomo cha Mulungu wathu kukhala chilakolako, . . .

⁹² Odzozedwa kale! Osati kuti Mulungu anakhala mmbuyomo pa mpandowachifumu, ndi kuti, “Ine ndidzamupulumutsa munthu uyu, Ine ndidzamataya munthu uyo.” Izo sizinali chomwecho! Mulungu anafa, ndipo pamene Yesu anafa, chitetezero chinaphimba dziko lapansi lonse kwa munthu aliyense. Koma Mulungu, mwa kudziwiratu. . . Osati kuti Iye akufuna. . . Iye sakufuna kuti aliyense ataike. Iye ankafuna aliyense kuti apulumutsidwe. Icho chinali Chake—icho chinali cholinga Chake Chamuyaya. Koma ngati Iye anali Mulungu, Iye anamudziwa yemwe akanati ndi yemwe akanati asadzapulumutsidwe. Ngati Iye akanati asadziwe, ndiye Iye

sanali Mulungu wopandamalire. Chotero Baibulo limaphunzitsa zimenezo. Kuti ife tikhoza . . .

⁹³ Ngati ife tikanakhala nayo nthawi yoti titembenuzire uku mu Aroma, mutu wa 8, ndipo inu mukhoza kuziwerenga izo. Aroma, mutu wa 9, malo ena ambiri mu Baibulo. Aefeso, mutu wa 1. Ndipo inu mukhoza kuwona kuti kusankha kwa Mulungu, kuti kuime motsimikizika, Mulungu anapereka pangano mopanda mangawa. Iye anamutumiza Yesu kuti adzawafere iwo omwe Iye anawadziwiratu. Mwaona?

⁹⁴ Osati kungonena kuti, “Chabwino, inu mukuti Mulungu sakudziwa ngati iye ati adzapulumutsidwe kapena ayi?” Mulungu anadziwa kuti inu mukanati mudzapulumutsidwe, kapena ngati inu mudzatero kapena ayi, dziko lisanayambe nkomwe, kapena Iye sanali Mulungu.

⁹⁵ Kodi inu mukudziwa chomwe mawu oti *infinite* amatanthauza? Yang’anani pa . . . tayang’anani mu dikishonare ndi kupezamo chomwe mawu oti *infinite* amatanthauza. Bwanji, Iye anadziwa utitiri uliwonse womwe ukanati udzakhalepo konse pa dziko lapansi, ntchentche iliyonse, tongole aliyense, nyongolosi iliyonse. Iye anazidziwa izo zisanadze nkomwe mu kukhalapo, kapena Iye sanali Mulungu. Ndithudi, Iye anazidziwa izo. Chabwino.

⁹⁶ Ndiye, mmenemo, Mulungu sakanakhoza—sakanati, “Ine ndidzakutengani *inu*, ndi kukutumizani inu ku hade; ndipo ine ndidzakutengani *inu*, ndi kukutumizani inu Kumwamba.” Mulungu ankafuna inu nonse kuti mudzapite Kumwamba. Koma mwakudziwiratu Iye anadziwa kuti mmodzi akanadzakhala ali shyashya, ndipo winayo akanadzakhala ali njonda ndi Mkhristu. Mwaona? Chotero Iye anachita kumutumiza Yesu kuti adzafe, kuti adzamupulumutse munthu uyo yemwe Iye anamudziwiratu yemwe ankafunayo kuti apulumutsidwe. Kodi inu mwamva zimenezo?

Tsopano penyani apa:

Malemba mosakaika amatiuza ife kuti awa ndi iwo omwe sati adzapulumutsidwe.

55. Chotero ngati chitetezero chinawaphimba onse . . . mtundu wonse wa Adamu, ndipo ena anataika chifukwa iwo sanadzipangitse kupezeka pa lonjezolo, kapena choperekedwa, sakanati, . . . akakhoze . . . afulu . . . kodi iye . . . idzakhala ili mphamvu yayikulupo kuposa madongosolo Amuyaya ndi zolinga za Mulungu Wamphamvuzonse? Kodi izo zikanakhala ziri . . . (Munthuyo tsopano, pa funso lachiwiri ili, ilo likufunsa . . .) . . . Kodi munthu sakanati akhale mwakufuna kwayekha kukhala mphamvu yopambanirapo kuposa madongosolo Amuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?

⁹⁷ Ayi, m'bale wanga kapena mlongo. Ndithudi ayi! Palibe chinthu china champhamvu mochulukirapo... Kufuna kwa munthu sikungakhoze konse kufanizitsidwa ndi—cholinga Chamuyaya cha chiweruzo cha Mulungu. Izo sizingakhoze kukhala ziri, mwaona.

⁹⁸ Tsopano, funso lanu loyamba linali lokhoza. Funso lanu lachiwiri sizingakhoze kukhala ziri, mzanga. Chifukwa onani, onani momwe izo zalembedwera apa, mwaona: “Kodi chifuniro chayekha cha munthu sichikanakhoza kukhala mphamvu yaikulupo kuposa dongosolo Lamuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?” (Bwanji, ndithudi ayi. Chingakhoze bwanji chifuniro cha munthu kukhala mphamvu yaikulupo kuposa cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse? Ndipo munthu mu chikhalidwe chake chachithupithupi pakufuna chimene iye akuchifuna, champhamvu mochulukira kuposa chomwe Mulungu Wamuyaya, wangwiro akanakhoza kukhala ali? Ndithudi ayi! Izo sizingakhoze kukhala, mwaona. Mulungu Wamuyaya, Yemwe cholinga chake ndi changwiro, inu munganene bwanji kuti—munthu wachithupithupi apa, ziribe kanthu momwe aliri wolungama (ndipo iye akhoza kukhala ali), zolinga zake simungakhoze mwanjira iliyonse chuzifanizitsa ndi izi: c—cholinga cha Mulungu Wamuyaya ndi Wamphamvuzonse.

⁹⁹ [Mlongo akuyankhula kuchokera kwa omvetsera—Mkonzi.] Inde. [“Ine ndikupepesa. Ine ndimangofuna kuti ndifunse funso, n—ndipo mwamvetsa molakwika zomwe ine ndimatanthauza apo.”] Eya, chabwino, mlongo. [“Ine sindimakhulupirira nkomwe izo, ine ndimatanthauza ‘cholinga Chamuyaya cha Mulungu chikuposa kudzisankhira kwa munthu.’”]

¹⁰⁰ Ndiko kulondola. O, chabwino, i—ine ndaziwerenga izo molakwika ndiye, mwaona. Chabwino. Inde, inu mukulondola ndendende apo, mlongo. Ine sindimadziwa kuti ilo linali lanu—funso lanu. Chabwino. Koma, onani, pamene ine ndinafika apa, onani, . . . Tsopano ndiloleni ine ndiwone, “Kuphimba mtundu wonse wa Adamu, ndipo ena anataika chifukwa iwo sanadzipangitse kupezeka ku—choperekedwacho, kodi chifuniro chayekha cha munthu sichingakhale cha mphamvu yaikulupo kuposa madongosolo Amuyaya ndi cholinga cha Mulungu Wamphamvuzonse?” Mwaona, i—ine ndinatanthauzira molakwika lingaliro lanu apo. Inde, cholinga Chamuyaya cha Mulungu Wamphamvuzonse. Chabwino, izo zikukhazikitsa icho.

¹⁰¹ Ine ndikuganiza aliyense wamvetsa izo. Ngati muli, kwezani inu manja anu. N—ndicho cholinga Chamuyaya cha Mulungu Wamphamvuzonse, ndithudi chikanakhala patali kuposa—patali kuposa chomwe munthu angakhoze kuchita.

Tsopano:

56. Ine sindiri kumvetsa kuwala kwa pa ubatizo wa madzi, mu mutu wa 28...ndime ya 19, ya Mateyu. Kodi izi zikutanthauza chiani?

¹⁰² Chabwino, tsopano, mwinamwake izi sizinditengera ine kupitirira miniti yokha. Ndipo tiyeni tikhale ndi wina ati atembenuze ndi ine ngati inu mungafune, ku Mateyu, mutu wa 28, ndi ndime ya 19. Ndipo ife tizipeza, basi chomwe munthu ali...twente-faifi...Tsopano, Izi zikupangani inu kukhala wamphamvu ngati inu muti mungokhala ndi Izo. Zi—ziri bwino, inu mukuona. Uwu si uvangeli, koma Ndi...

¹⁰³ Tsopano ife tiri...Tsopano apa ndi pamene anthu amayesera kumati, “Muli kutsutsana mu Baibulo.” Tsopano, ine ndikufuna winawake kuti atsegule ku...nane Mateyu 28:19. Kapena, ayi, ine ndikufuna winawake...Mateyu 28:19. Ine ndikufuna winawake kuti atsegule ku Machitidwe 2:38. Inu muli nalo Baibulo lanu apo, M'bale Neville?

¹⁰⁴ Ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziwerengere nokha tsopano. “Ndipo ine ndikusonyezani inu kutsutsana kosamalitsa mu Baibulo. Ndipo zimene—Baibulo...Anthu amati ‘Baibulo silimadzitsutsa Lokha,’ ine ndikufuna inu kuti muzitenge izi molingalira.”

¹⁰⁵ Ndipo izi zimawapangitsa aphunzitsi kuchita imvi. Koma I—Izo ndi zophweka. Tsopano ine ndiwerenga Mateyu 28:19, inu munditsatire ine. Ndipo ena a inu muli ndi Machitidwe 2:38, mukhale napo mokonzekera. Ine ndiyambira ku ndime ya 18, uwu ndi mutu wotsekera wa Mateyu:

Ndipo Yesu anadza ndipo anayankhula kwa ophunzira ake...anayankhula kwa iwo, kuti, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa ine kumwamba ndi dziko lapansi. (mphamvu za Atate ziri kutino?)

¹⁰⁶ Ngati mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zapatsidwa kwa Yesu, Mulungu anali wopanda mphamvu ndiye sichoncho Iye? Kapena kodi Iye ankangonena nthano? Kodi Iye anali akuserwula? Iye ankatanthauza Izo! Kodi inu simukukhulupirira kuti Iye ankatanthauza Izo? Chabwino, ngati mphamvu zonse zaperekedwa kwa Iye, mphamvu ya Mulungu ili kuti ndiye? Iye anali Mulungu! Ndizo ndendende. Ndi chinthu chokha chiripo kwa izo. Ndi basi zonse zomwe zinalipo. Mwaona, Iye anali Mulungu; kapena mwina pali winawake wakhala uko, yemwe anali ndi mphamvu, alibe izo panonso. Mwaona? Chotero inu simungati—inu simungati musokoneze Izo. Ife tizipeza izo umu momwe pa chinthu chomwe ichi apa. Chabwino:

...Mphamvu zonse kumwamba ndi pa dziko lapansi ziri...kumwamba ndi pa dziko lapansi.

Pitani inu chotero, . . . kaphunzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera:

Kuwaphunzitsa iwo kuti azisunga zinthu ziri zonse zomwe ine ndakulamulirani inu: . . . taonani, ine ndiri ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka ku mathero a dziko.

¹⁰⁷ Machitidwe 2:38, tsopano winawake awerenge. Dikirani miniti yokha. Machitidwe mutu wa 2, ndime ya 38. Tsopano, mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano, ndipo ingokhalani mopirira, ndipo ife tiwona tsopano. Tsopano, awa ndi masiku khumi kenako Yesu atawauza kale iwo tsopano, Mateyu 28:19, “Pitani chotero, kaphunzitseni mafuko onse, nkuwabatiza iwo mu dzina la Atate, la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.”

¹⁰⁸ Tsopano, Petro, masiku khumi kenako . . . Iwo sanalalikire konse ulaliki wina. Iwo anapita mmwamba mu chipinda chapamwamba ku Yerusalemu, ndipo anakadikira mmenemo (kwa masiku khumi) kuti Mzimu Woyera udze. Ndi angati akudziwa izo? Mu malo awa. Apa pali Petro, Petro ali ndi mafungulo a ku Ufumu. Chabwino, ife tiwona zomwe iye ati achite. Mateyu . . . kapena ine ndikutanthauza Machitidwe 2, tiyeni titenge ndime ya 36:

Chotero nyumba yonse ya Israeli idziwe motsimikiza, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyeyu, yemwe inu . . . munamupachika, zonse Ambuye ndi Khristu.

“Zonse Ambuye ndi Khristu.” Palibe, zodabwitsa kuti mphamvu zonse kumwamba ndi pansi zapatsidwa kwa Iye.

Tsopano pamene iwo anamva izi, iwo analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati kwa Petro ndi . . . atumwi ena onsewo, Amuna ndi abale, kodi ife tichite chiani?

Petro anayankha . . . Petro anati kwa iwo, Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

¹⁰⁹ “Tsopano, apo pali kutsutsanako. Mateyu anati, ‘kabatizeni mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera,’ ndipo Petro anati mu Machitidwe 2:38, masiku khumi kenako, ‘Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.’”

¹¹⁰ Ndiye nthawi yotsatira yomwe kulapa kunatchulidwa—kunayankhulidwa . . . kapena ubatizo, mu Baibulo, ndi Machitidwe—mutu wa 8, pamene Filipino anapita uko nakalalikira kwa . . . k—kwa Asamaria. Ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, ndipo iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

¹¹¹ Nthawi yotsatira yomwe iwo unayankhulidwapo, panali pamene Amitundu anaulandira Iwo, Machitidwe 10:49:

Ndipo *pamene Petro . . . anali kuyankhula mawu awa, taonani, Mzimu Woyera unagwera pa . . . iwo . . . ndipo anawamva iwo.*

Pakuti anawamva iwo akuyankhula mu malirime, ndi kumamukuza Mulungu. Ndiye Petro anati,

Kodi munthu angaletse madzi, poona kuti awa . . . alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pa chiyambi?

Ndipo iye anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu dzina la Ambuye Yesu Khristu.

¹¹² Tsopano ndiloreni ine ndikhale ndi chinachake apa, kuti ndingokusonyezani inu chinachake chaching'ono mokuti inu musadzaziwale izo; ndikupangirani kalongosedwe kakang'ono. Ine ndiika . . . Ndi mitundu ingati . . . mafuko a anthu alipo mu dziko? Alipo atatu: anthu a Ham, Shemu, ndi Yafeti. Ndi angati amadziwa zimenezo? Ife tinabwera kuchokera kwa ana aamuna atatu a Nowa awo. Anthu a Hamu, anthu a Shemu . . . Anthu a Yafeti ndi Angelezi achi saxoni, anthu a Shemu ndi . . . Timibadwo titatu, ndiwo: Myuda, Wamitundu, ndi wa theka Myuda ndi Wamitundu. Tsopano, zindikirani, pamene ipo . . . ndipo *uyu* ndi Hamu . . . Shemu, Hamu, ndi Yafeti.

¹¹³ Tsopano, nthawi yoyamba yomwe ubatizo unayamba wayankhulidwapo, unayankhulidwa ndi Yohane M'batizi. Ndi angati akudziwa izo kuti nzoona? Chabwino, ine ndiziyika *izi* patali apa, cha apa, Yohane M'batizi. Ndipo Yohane ankawabatiza anthu mu mtsinje wa Yordani, kuwalamulira iwo kuti ayenera kulapa ndi kukonza ndi Mulungu, ndi kugulitsa katundu wawo, ndi kuwadyetsa osauka, ndi asilikari kuti azikhutitsidwa ndi ndalama zawo, ndi kuti afike pabwino ndi Mulungu. Ndi angati akuzidziwa izo? Ndipo iye ankawabatiza iwo mu mtsinje wa Yordani, osati kuwakonkha iwo, osati kuwatsanulira iwo, koma kuwamiza iwo! Ngati inu simukuzikhulupirira Izo, pano pali lexicon, fufuzanimo ngati iyo isali *baptizo*, chomwe chiri “kubatiza, kumizidwa, kuvindikiridwa, kukwiriridwa.” Tsopano, nthawi yoyamba yomwe ubatizo unayamba wayankhulidwapo, panali pamenepo.

¹¹⁴ Nthawi yachiwiri yomwe ubatizo unayamba wayankhulidwapo, Yesu anawulamulira iwo, Mateyu 28:19.

¹¹⁵ Nthawi yotsatira ubatizo unayankhulidwapo, panali pa Machitidwe 2:38.

¹¹⁶ Nthawi yotsatira ubatizo unayankhulidwapo, munali mu Machitidwe mutu wa 8.

¹¹⁷ Nthawi yotsatira ubatizo unayankhulidwapo, munali mu—mutu wa 10 wa Machitidwe.

118 Ndiyeno ife tinabwera kuchokera ku nthawi yomwe Yesu anati, apa, “Pitani inu chotero, kawaphunzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, Mzimu Woyera.”

119 Tsopano tiyeni tiliwongole lemba ili, choyamba. Ine ndakuuzani inu kuti “mulibe Lembam limodzi mu Baibulo lomwe liti lidzatsutsane ndi limzake.” Ine ndikufuna kuti inu mulibweretse ilo kwa ine. Ine ndafunsa izo kwa zaka twentisikisi, ndipo ine sindinalipeze ilo panobe. Palibe Lembam lomwe limas- . . . Ngati ilo limatsutsa Iwo, ndiye ndi zinthu zolembedwa ndi anthu. Ayi, bwana, mulibe kutsutsana mu Baibulo!

120 Tsopano izi inu munati, “Nanga bwanji izo?”

121 Apa waima Yesu akuti, “Pitani inu chotero, kukawaphunzitsa mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera.”

122 Ndipo Petro nkutembenuka apo pomwe, nkuti, “Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.”

123 “Ndi uko kutsutsana kwanu.” Zikuwoneka ngati choncho. Tsopano, ngati inu mukuwerenga ndi malingaliro achithupithupi, ndipo osati ndi mtima wotseguka, uko kukhala kutsutsana.

124 Koma ngati inu muti muwerenge Iwo ndi malingaliro otseguka, “Mzimu Woyera wazibisa izi kwa maso a anzeru ndi aluntha,” Yesu ananena chomwecho, ndipo anathokoza Mulungu chifukwa cha izo, “ndipo wawululira Izi kwa makanda omwe angati aphunzire.” Ngati inu muli ndi malingaliro, ndipo osati malingaliro odzikonda, koma mtima wololera kuti muphunzire, Mzimu Woyera ukuphunzitsani inu zinthu izi.

125 Tsopano ngati izo sizikufanana. . . Inu mukati, “Inu mukudziwa bwanji kuti inu mukulondola?” Chabwino, izo zikufanana ndi Lembam lina lonse. Ngati inu simutero, inu muli ndi kutsutsana kwapoyera apa.

126 Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu funso. Uwu ndi mutu wotsiriza wa Mateyu. Ine ndizitenga izo mwamawonekedwe aang’ono, chotero kuti aliyense wa inu. . . ana azimvetse Izo.

127 Mwa chitsanzo, ngati inu mukanawerenga nkhani ya chikondi, ndipo kumbuyo kwa iyo ikuti, “Ndipo Maria ndi Yohane anakhala mosangalala kuyambira pamenepo.” Chabwino, inu mukanadabwa yemwe Yohane ndi Maria anali omwe anakhala mosangalala kuyambira apo. Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mudziwe yemwe Yohane ndi Maria ali, inu kuli bwino mupite koyambirira kwa bukhu ndi kukapeza yemwe Yohane ndi Maria ali. Ndiye nkubwerera apa ndi kudzapeza yemwe Maria anali, ndi banja lomwe iye anachokerako; ndi yemwe Yohane anali, ndi banja lomwe iye anachokerako, ndi

lomwe dzina lake linali, ndi momwe iwo anakwatirirana, ndi zonse izo. Nkulondola uko?”

128 Chabwino, icho ndi chinthu chofanana pa kuwerenga Baibulo apa. Pamene...Penyani, Yesu sanati konse, “Pitani kawabatizeni anthu mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, mu dzina la Mzimu Woyera,” momwe anthu autatu amabatizira. Palibe Lemba la izo mu Baibulo. Iye sanati konse, “Mu maina (m-a-i-n-a), maina” a Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

129 Iye anati, “Mu (d-z-i-n-a) dzina,” limodzi. Yang’anani pa Baibulo lanu ilo ndi kupeza ngati uko kuli kulondola, Mateyu 28, “Mu *Dzina*.”

130 Osati “mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, . . .” umo ndi momwe mlaliki wautatu amabatizira. “Mu dzina la Atate, mu dzina la Mwana, ndi mu dzina la Mzimu Woyera.” Izo mulibemo nkomwe mu Baibulo.

131 “Ndiye mu dzina . . .” Inu mukuti, “Chabwino, ndiye mu dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Ndiye pali dzina linalake apo.

132 Chabwino, kodi Atate ndi dzina? Ndi angati akudziwa kuti Atate si dzina. Atate ndi udindo. Mwana si dzina. Ndi angati akudziwa kuti Mwana si dzina? Ndi atate angati ali muno? kwezani dzanja lanu. Ndi ana angati ali muno? kwezani manja anu. Chabwino, ndi ndani wa inu dzina lake ali “mwana”? Ndi ndani wa inu dzina lake ali “atate”? Chabwino, Mzimu Woyera si dzina. Mzimu Woyera ndi chimene Iwo uli. Ndi anthu angati ali muno? kwezani dzanja lanu. Mwaona? Ndi inu apo, Mzimu Woyera ndi chomwe Iwo uli. Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, palibe limodzi la iwo liri maina; palibe dzina kwa ilo.

133 Chabwino, ndiye, ngati Iye anati, “Zibatizani mu Dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera,” ife kulibwino tipite mmbuyo ndi kukapeza yemwe Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali. Tiyeni titembenezire mmbuyo ku mutu wa 1 wa Mateyu ndiye, tikawone Yemwe munthu uyu anali yemwe ife tikuyenera kumabatiza mu dzina liti. Ndipo ife tiyambira tsopano ndi Mateyu, mutu wa 1, ndi ndime ya 18. Werengani mwacheru, nonse inu.

134 Tsopano, inu amene munafunsa funsoli, ine ndikufuna kuti ndipereke kalongosoledwe kakang’ono apa. Tsopano ine ndikuti ndiike zinthu zitatu apa chotero kuti inu mumvetse bwino, (ndipange kalongosoledwe) Mabaibulo awa ndi mabuku, kuti ndipangire kalongosoledwe.

135 Chabwino, ine ndikufuna kuti inu mundiyang’ane ine mwacheru, ndipo aliyense azinditsatira ine tsopano. Tsopano, *uyu* apa ndi Mulungu Atate. *Uyu* apa ndi Mulungu Mwana. *Uyu* apa ndi Mulungu Mzimu Woyera. Tsopano, ndi angati akumvetisa? Ine munene izo monditsatira ine. Ndi ndani uyu apa?

[Osonkhana ati, “Mzimu Woyera”—Mkonzi.] Mzimu Woyera. Ndi ndani ali apayu? [Osonkhana ati, “Atate”—Mkonzi.] Ndi ndani uyu apa? [Osonkhana ati, “Mwana”—Mkonzi.] Tsopano, umo ndi momwe autatu amakhulupirira izo. Mwaona, izo zimatipangitsa ife achikunja, aawisi basi momwe iwo angakhoze kukhalira.

¹³⁶ Myuda; ndi chifukwa inu simungakhoze kuchita kanthu ndi Myuda. Iye anati, “Inu simungakhoze kumudula Mulungu mu zidutswa zitatu ndi kumupereka Iye kwa Myuda.” Koma, ndithudi ayi, inu simungatero kwa ine ngakhalenso. Mwaona? Ayi, bwana. Iye ndi Mulungu mmodzi. Ndizo ndendende. Osati Amulungu atatu. Tsopano zindikirani momwe—momwe—momwe Izo zirili zophweka.

¹³⁷ Tsopano ife tikuti tipeze. Tsopano, ndi ndani ali... *Uyu* ndi ndani? Ena ayankhulapo tsopano. Mulungu Mwana. Ndi kulondola uko? *Uyu* ndi Mwana. Chabwino, ndiye atate Ake ndi Mulungu. Nkulondola uko? Ndi angati akukhulupirira kuti atate Ake ndi Mulungu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndi angati akukhulupirira kuti Mulungu ndi Atate a Yesu Khristu? Chabwino.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: . . .

¹³⁸ Tsopano ife tikuti tibwerere mmbuyo kuti tikapeze omwe Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali, omwe Mateyu anati “muzikabatiza mu Dzinalo.” Mwaona, Dzina; osati maina tsopano, chifukwa iwo sangakhoze kukhala maina, chifukwa palibe dzina apo.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene . . . mayi wake Maria anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, iwo asanabwere palimodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa Mulungu Atate. (Kodi Baibulo limanena chomwecho? Kodi Baibulo limati chiani?) . . . iye anapezeka ali ndi mwana wa Mzimu Woyera.

¹³⁹ Ndiye n’ndani mwa *awa* ali atate Ake? Tsopano, Baibulo linanena kuti *awa* ndiwo atate Ake, ndipo Yesu ankanena kuti *awa* anali atate Ake. Tsopano, ndi uti ali atate Ake? Tsopano, ngati iye anali ndi atate awiri, tsopano nanga bwanji izo? Ngati Iye anali nawo atate awiri, Iyeyo ndi mwana wapathengo.

¹⁴⁰ Tsopano tiyeni tingowerenga mopitirira pang’ono:

Ndiye Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama, sanali kulolela kuti amunyazitse iye kugulu, koma analingalira kuti amusiye iye mwamseri.

Koma pamene iye anali kulingalira pa zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto, nati, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope kudzitengera Maria mkazi wako: pakuti icho

chomwe chiri kuyembekezedwa mwa iye ndi cha...
[Osonkhana ati, “Mzimu Woyera”—Mkonzi.]

141 Chiani? Mzimu Woyera? Chabwino, Atate angakhoze bwanji kukhala atate ake, ndipo Mzimu Woyera nkukhala atate Ake pa nthawi yomweyo? Tsopano, Iye anali ndi atate awiri ndiyetu, ngati uko kuli kulondola. Ayi, bwana! Mzimu Woyera NDIWO Mulungu. Mzimu Woyera NDIWO MULUNGU. Kotero Mulungu ndi Mzimu Woyera ali Munthu yemwe yemweyo, kapena Iye anali ndi atate awiri.

142 Mukuona, ife tipeze yemwe *Yohane ndi Maria* ali, pakapita kanthawi. Chabwino, ife tipeza ngati Petro ndi Mateyu ankayesera kuti azitsutsana wina ndi mzake kapena ayi, tiona ngati Lemba limadzitsutsa Lokha. Ndi kusowa kwa kumvetisa kwauzimu. Ndiko kulondola.

Koma pamene iye anali kuganizira pa izi...

143 Ine ndapatenga apo, ndime ya 20. Tsopano ya 21:

Ndipo iye adzabala mwana...(Munthu uyu, yemwe anali wa Munthu Mmodziyo, Mulungu,...
ndipo iwe udzamutcha dzina lake...(chiani?)
[Osonkhana ayankha, “YESU”—Mkonzi.]...*pakuti iye adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo.*

...izi zonse zinachitidwa, kuti...zikhoze kukwaniritsa zomwe zinayankhulidwa ndi Ambuye ndi mneneri, kuti,

Taonani, namwali adzakhala ndi pakati, ndipo adzabala mwana, ndipo iwo adzamutcha dzina Lake Emanuele, ...mwa kutanthauzira, Mulungu nafe.

144 Kotero kodi *Yohane ndi Maria* anali ndani omwe anakhala mokondwa nthawizonse mpakana? Anali ndani yemwe anati, “Pitani inu chotero, kukawaphunzitsa mafuko onse, muzikawabatiza iwo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera”? Atate anali ndani? Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera? [Winawake akuti, “Yesu”—Mkonzi.] Ndithudi, iye anali. Ndithudi, palibe kutsutsana pa izo. Osati pang’ono. Izo zikungowongola Lemba bwino. Iye anali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Mulungu anali (Emanuele) akukhala ndi ife, mu kachisi wa thupi lotchedwa “Yesu.”

145 Tsopano, kuphunzitsa kwa umodzi kwa mpingo wa Umodzi, ine ndithudi ndimatsutsana ndi izo, kuganiza kuti Yesu ndi mmodzi monga chala chanu chiri chimodzi. Iye ankayenera kukhala nawo atate. Ngati Iye sakanatero, Iye akanakhoza bwanji kukhala atate wa Iye yekha? Ndipo ngati Atate Ake anali munthu monga autatu amanenera, ndiye iye anabadwa mwa kubadwa kwa mchigololo ndi atate awiri. Kotero, inu mukuona, ndinu nonse olakwa potsutsana. Mwaona?

146 Koma Choonadi cha izo ndi ichi, kuti zonse Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, ndi Umunthu umodzi. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...wa kukhala mu kachisi wa thupi, kuti achotse tchimo mu dziko. Ndendende kulondola, “Mulungu ali nafe.” Tsopano, chotero, pamene Mateyu 28:19... .

147 Tsopano, inu fufuzani Malemba, ndipo pamene inu mungakhoze kupeza pamene munthu mmodzi mu Baibulo... (tsopano ganizani za izo, tsopano musati mulole izi kuti zidutse pamwamba pa inu)...pamene munthu mmodzi mu Baibulo anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate,” ndi la “Mwana,” ndi la “Mzimu Woyera,” mubwerere kwa ine ndi kudzandiuza ine kuti ndine wachinyengo, ndipo ine ndiika chizindikiro pa nsana wana ndi kumayenda kudutsa mu mzinda. Izo siziri mu Malemba, kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso. Koma munthu aliyense mu Baibulo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu!

148 Inu mukuti, “Dikirani miniti, mlaliki. Nanga bwanji Yohane? Iye sanali kubatiza mu dzina lirilonse nkomwe!”

149 Chabwino, ife tipeza zomwe zinkachitika; tiyeni titembuzire cha k—ku—Machitidwe, mutu wa 19. Ndi pamene ife tikuwapeza ophunzira a Yohane. Munthu aliyense onse anali kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, kupitirira nazo tsopano mpaka ife tipeze gulu ili cha kuno. Machitidwe, mutu wa 19. Ndipo tiyeni tiyambe kuwerenga tsopano, ndipo ife tikuwapeza ophunzira a Yohane:

Ndipo zinafika pochitika, ...pamene Apollo (yemwe anali wazamalamulo, atatembenezidwa) anali ku Korinto, Paulo atadutsa ku magombe aku mtunda... Efeso: iye anapezako ophunzira ena, (iwo anali otsatira a Yesu)

150 Ngati inu muti mungozindikira mutu wammbuyowu tisanafike apo, iwo nkuti amakhala ndi nthawi yaikulu chotero mpaka iwo anali kufuula ndi kusangalala. Ndi angati akudziwa kuti izo nzoona? Ndipo Aquila ndi Priscilla anali nawo pa msonkhanowo. Ndipo Paulo ndi Sila anamenyedwa ndi kukwapulidwa, ndi kuikidwa mu ndende. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo anabwera mpaka kuno, ndipo anadzawapeza Aquila ndi Priscilla. Ndipo iwo anali ali ndi chitsitsimutso kumeneko ndi mlaliki wa Baptisti, dzina lake Apollo, yemwe anali kutsimikizira mwa Malemba kuti “Yesu anali Khristu.” Tsopano Paulo akumupeza iye:

...Paulo atadutsa ku magombe aku mtunda... Efeso: ...anawapeza ophunzira ena,

Iye anati kwa iwo, Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?...

151 Tsopano, iwe mzanga wokonedwa wa Chibaptisti, ngati izo sizikugwetsa—zopukusira za fioloje *yanu*, pamene inu mumati inu “munalandira Mzimu Woyera *pamene* inu mukhulupirira.”

152 Koma Paulo ankafuna kuwafunsa Achibaptisti awa, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* chikhulupirireni chanu?” Tsopano penyani zomwe iwo ananena:

... Ndipo iwo anati kwa iye, Ife tikudziwa... ngati kuli Mzimu Woyera konse.

Ndipo iye anati kwa iwo, Nkwa chiani... (tsopano, ngati inu mukufuna kuti mutenge lexicon yachi Griki apa, iyo ikusonyezani inu, “Mmotani momwe inu munabatizidwira?”)... Nkwa chiani... komwe inu munabatizidwira? Ndipo iwo anati kwa iye, Kwa Yohane mmbuyo kuno. Yohane anatibatiza ife.

153 Tsopano ine ndikufuna kuti ndifunse: Ngati inu mukanakhala nao ubatizo umenewo, kodi inu mukanakhutitsidwa nawo iwo? Munthu yemweyo yemwe anayenda ndi Yesu kupita mu mtsinje, ndipo anamubatiza Yesu Khristu, munthu yemweyo anali atawabatiza anthu awa. Ndiwo ubatizo wabwino ndithu: osati kukonkha, osati kutsanulira, koma kumiza mu matope a Yordani wakaleyo pa malo omwewo pomwe Yesu anabatizidwa. Ganizirani za izo.

154 Paulo anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?” Iwo... iye...

Iwo anati, “Ife tikudziwa... ngati pali Mzimu Woyera uliwonse.”

Iye anati, “Nanga inu munabatizidwa chotani?”

Iwo anati, “Ife tinabatizidwa kale.”

“Kodi inu munabatizidwa chotani?”

“Kwa Yohane!”

155 Tsopano penyani zomwe Paulo ananena. Penyani apa:

Ndipo iye anati kwa iwo, ... kodi inu munab-... Kwa Yohane... Ndipo iwo...

Ndiyeno Paulo anati, Yohane ndithudi ankabatiza... ubat-... kwa kulapa, kumati kwa... anthu... iwo akhulupirire pa iye yemwe anali nkudza pambuyo pa iye, pomwe pali, pa Yesu Khristu.

156 Mwaona, Yohane anali kungobatizira *kwa* kulapa, koma ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu ndi wa kuchotsedwa kwa machimo. Chitetezero chinali chisanapangidwe apo, machimo sakanakhoza kuchotsedwa. Tsopano... Ilo linali yankho chabe la ku chikumbumtima, monga pansu pa lamulo. Luka 16:16, anati, “Lamulo ndi aneneri zinalipo mpaka pa Yohane, chiyambireni apo Ufumu wakhala ukulalikidwa.” Tsopano penyani. Ndipo... Penyani:

Ndipo Paulo *anati kwa-* . . . (tsopano penyani) . . . *Kodi inu munalandira* . . .

157 Wa 5—ndime ya 5:

Ndipo *pamene iwo anamva izi, iwo anabatizidwa* (kachiwiri) *mu dzina la* . . . Yesu Khristu.

158 Nkolondola uko? Ndiye anthu awa, anthu mu Machitidwe 2, anabatizidwa mu Dzina la Yesu. Ayuda ankabatizidwa mu Dzina la Yesu. Amitundu ankabatizidwa mu Dzina la Yesu. Ndipo munthu aliyense mu Baibulo lonseli anali kubatizidwa mu Dzina la Yesu.

159 Tsopano kapezeni malo amodzi pomwe wina aliyense anayamba wabatizidwapo mwanjira ina iliyonse, ndipo ine ndibwerera kuno komwe ndi kudzakusonyezani inu pamene mpingo wa Katolika umavomerezera izo, ndi kunena kuti inu mumagwadira kwa izo. Ndipo amati, “Pakhoza kukhala pali Achiprotostantani ena omwe adzapulumutsidwa chifukwa iwo ali nazo pang’ono za ziphunzitso za Chikatolika, monga ngati ubatizo mu dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera’; kuti mpingo woyera wa Katolika uli nao ulamuliro wosintha chofunika icho kuchokera ku Dzina la Yesu, kupita ku ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,’ ndipo mpingo wa Chiprotostantani umazivomereza izo.” Uno sumatero, ine ndimakhala ndi Baibulo. Ine ndimalikhulupirira Baibulo.

160 Inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mumawalamulira anthu kuti abatizidwe mobwerezanso?” Mwamtheradi! Paulo anatero, apa.

161 Tsopano penyani, tiyeni titenge Agalatia 1:8, ndi kupeza zomwe Paulo ananena:

. . . ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, atalalikira uthenga wina uliwonse kwa inu . . . musiyeni iye akhale wotembereredwa.

162 Ndi inu apo, “Ngati ife kapena mngelo.” Ndipo Paulo, munthu yemweyo, anawalamulira anthu kuti abatizidwe mobwerezanso omwe anali ndi ubatizo wabwinoko kwambiri kuposa womwe inu mwakhala muli nawo, m’bale wanga; pakuti Yohane M’batizi anali msuweni wake yemwe wa Yesu, msuweni wachiwiri; kumubatiza msuweni wake yemwe mu mtsinje wa Yordani, ndipo anatembenuka apo ndi kuwabatiza ophunzira a Yohane. Ndipo Yesu anati, “Izo sizigwira ntchito!” kapena Paulo ananena Izo, ndipo anawalamulira iwo kuti abatizidwe mobwerezanso mu Dzina la Yesu Khristu iwo asanafike polandira Mzimu Woyera; iwo atafuula kale ndi kumutamanda Mulungu ndi kukhala nayo nthawi yaikulu, ali ndi chachikulu—chitsitsimutso chachikulu, ndi kutsimikizira mwa Baibulo (ndi fioloje yawo) kuti Yesu anali Khristu. Ndi angati akudziwa kuti

ilo ndi Lemba? Mutu wa 18. Ndithudi izo ziri. Apo inu muli. Koteru palibe funso kwa Izo.

163 Tsopano ndiroleni ine ndikupatseni inu poyambira papang’ono. Tsopano, iye sanapite konse kunja kwa dongosolo, koma mu Luka . . . Mateyu, mutu wa 16. Yesu, pamene iwo anali kubwera akutsika kuchokera m’phiri, Iye anati, “Ndi ndani yemwe anthu amati Ine Mwana wa munthu ndiri?”

164 “Ena akuti Ndinu ‘Eliya,’ ndipo ena akuti Ndinu ‘mneneri,’ ndipo ena akuti Ndinu ‘*ichi, icho.*’”

165 Iye anati, “Koma inu mukuti ndi ndani?”

166 Petro anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

167 Penyani! “Wodala ndiwe, Simoni Bar Yona (mwana wa Yona), thupi ndi mwazi sizinaululire konse Izi kwa iwe.” Amen!

168 Onani, Izo ziyenera kubwera mwa vumbulutso lauzimu. Thupi ndi mwazi sizinamuuze konse Abele kuti iye anali kulakwitsa (Kaini, kuti iye anali kulakwitsa), sanamuuze konse Abele kuti “Kaini anali kulakwitsa.” Koma Ilo linali vumbulutso lomwe Abele anali nalo, “Iwo anali magazi!” Ife tikubwera ku funso ilo mu maminiti pang’ono. Iwo anali magazi, osati zipatso, zomwe zinati chotsa ife ku Munda wa Edeni. “Iwo anali magazi,” ndipo Abele, mwa vumbulutso lauzimu . . . anaululidwira ndi Mulungu kuti anali magazi. Ndipo iye, “Mwa chikhulupiriro” Ahebri 11:1 amati, “Iye anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri kuposa Kaini. Chomwe, Mulungu anailandira nsembe yakeyo.” Ndi inu apo. Mwaona, iye anaipereka iyo mwa chikhulupiriro, mwa vumbulutso.

169 Tsopano penyani, “Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe,” (kudutsa mpaka kwa Ambuye Yesu) “koma Atate anga omwe ali Kumwamba awululira Izi kwa iwe. Ndipo pa thanthwe ili (vumbulutso la Yesu Khristu) . . . Pa thanthwe ili Ine ndimangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzuluka Iwo.” Ndi zomwe Iye ananena. Lauzimu vumb- . . . “Ndipo Ine ndikuti iwe ndiwe Petro, ndipo Ine ndipereka kwa iwe mafungulo a Ufumu. Ndipo chirichonse . . . Chifukwa iwe uli ndi khomo lotseguka lauzimu pakati pa kuno ndi Kumwamba. Thupi ndi magazi: iwe sunatengeremo seminare, iwe sunatenge za sukulu, iwe sunatenge m—m—maphunzira a fioloje. Koma iwe unadalira pa Mulungu, ndipo Mulungu anaululira Izo kwa iwe, ndipo ndizo mwamtheradi Malemba omveka amene akumangirizira Izo palimodzi. Ine ndikuti iwe ndiwe Petro, ndiko kulondola, ndipo Ine ndipereka kwa iwe mafungulo; ndipo chimene iwe umanga pa dziko lapansi, Ine ndizichimanga icho Kumwamba; chimene iwe uzichimasula pa dziko lapansi, Ine ndizichimasula icho Kumwamba.”

170 Ndipo Petro anali wowayankhulira pa Tsiku la Pentekoste, pamene iwo onse ankachita mantha kuti ayankhule, iye anayankhula nati, “Inu amuna amu Yudea ndi inu okhala mu Yerusalemu, lolani ichi chidziwike kwa inu ndipo mvetserani kwa Mawu anga. Awa sanaledzere monga inu mukulingalira, powona kuti lino ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli. ‘Zidzafika pochitika mu masiku otsiriza,’ akutero Mulungu, ‘Ine ndidzatsanulira Mzimu Woyera pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi azidzanenera. Ndipo pa adzakazi anga, antchito anga aakazi, Ine ndidzatsanulirapo za Mzimu Wangwa. Ndipo Ine ndidzazasonyeza zizindikiro mmiyamba umo ndi padziko apo, ndi mizati ya utsi ndi chifunga. Zidzafika pochitika Tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye lisanadze, kuti aliyense yemwe ati azidzaitanira pa Dzina la Ambuye azidzapulumutsidwa.’” Ndi inu apo. O, mai.

171 “Siyani ine ndiyankhule momasuka kwa inu za mbadwa Davide,” iye anatero, “iye anafa ndipo anaikidwa, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka lero. Chotero, pokhala mneneri, iye anawona. . . anamuwoneratu Iye pa dzanja Lake lamanja, ‘Ndipo Ine sindidzasunthidwa. Kuwonjezera apo mnofu Wangwa udzapuma mwa chiyembekezo chifukwa Iye sadzaisiya solo Yanga mu hade, ngakhalenso sadzalola Woyera Wake Uyo kuti awone chivundi.’”

172 “Ndipo Davide pano anafa,” iye anati, “ndipo anaikidwa, ndipo manda ake ali ndi ife tsiku lino. Koma pokhala mneneri, iye anawoneratu kudza kwa Wolungama Uyo, yemwe Mulungu wamupanga kukhala zonse Ambuye ndi Khristu.” O, mai. Ndi awo Malemba anu. Ndi icho chinthucho. Ndi chimenecho.

173 Tsopano ife tikupeza apa, ndiye, kuti njira yolondola, ndipo njira yeniyeni, ndi njira yokha yomwe inayamba yadzozedwera. . . Ndipo Petro anali nao mafungulo, ndipo pa tsiku limene iye analalika, iwo anati. . . Tsopano tayang’ana, pano pali Mpingo woyambirira. Inu Akatolika mvetserani kwa Izi. Inu Achicampbello mvetserani kwa Izi. Inu Abaptisti ndi Amethodisti mvetserani kwa Izi. Ndi inu Achipentekoste mvetserani kwa Izi. Mpingo wa Mulungu, Anazerini, Pilgrim Holiness, mvetserani kwa Izi.

174 Petro anali nawo mafungulo, ndipo iye anali nawo ulamuliro, kapena Yesu ananama. Ndipo nkosatheka kuti Iye aname, “zinthu ziwiri zosatheka, ndi kosatheka kuti Mulungu aname.” Iye anali nawo mafungulo. Yesu anamupatsa iye mafungulo. Pamene Iye anauka pa—pa tsiku lachitatu monga choncho, Iye anali nawo mafungulo a imfa ndi hade, koma osati mafungulo aku Ufumu. Petro anali nawo iwo! Ndiko kulondola ndendende.

175 Ndipo tsopano samalira, Petro, iwe uli nawo mafungulo akulendewera pambali yako, ndipo iwe ukulalikira. Funso

labwera, otembenuka mtima oyamba a mpingo watsopano. Mpingo wa Chikhristu woyambirira. Tsopano Katolika, tsopano Abaptisti, Amethodisti, Apresbateria, kodi inu muli pa chiphunzitso cha Mpingo Watsopano? Fufuzani ngati inu muli.

... Amuna *ndi abale, kodi ife tingakhoze kuchita chiani?*

... *Petro* anaimirira apo ndipo *anati...Lapani, ... aliyense wa inu...* (samalira apo, mnyamata; momwe iwe uti uwaikire mafungulo awo apa, Khristu awaika iwo Kumwamba)... *Lapani*, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa *mu dzina la Yesu Khristu...* (ndi momwe inu mumalowera mu Izi)... *kwa chikhululukiro cha machimo* anu, *ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.*

¹⁷⁶ Mafungulo anamveka “kiliki” kuno, ndipo iwo anamveka “kiliki” Uko. Ndi chifukwa chake ophunzira a Yohane anachita kubwera ndi kudzabatizidwa, kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu (iwo asanapite Kumwamba), nalandira Mzimu Woyera. Iye anasunga Mawu Ake. Kotero izo sizikusokonezani inu tsopano, sichoncho izo? Mwaona? Ndithudi, Mateyu 28:19 anali maudindo, osati Dzina.

¹⁷⁷ Chabwino, kodi ife tiri nayo nthawi ina yochuluka bwanji? Kodi ife tingakhoze kukhala ndi maminiti ena fifitini owonjezra kuti tiyankhe mafunso angapo ena mofulumira kwenikweni? Tingatero ife? Chabwino, ife tifulumira mwamsanga ndithu. Ine ndiri nawo awiri pansu apa mmusimu, ine ndimafuna kuti ndiwatenge mofulumira, alumikizane umo momwe ndi izi, ngati ine ndingathe. Ndiye ine ndikhoza kudzawatenga ena onsewo Lamlungu mmawa.

57. Kodi Kaini anali mphukira ya serpenti? (Ili ndi labwino lake.) Ngati ziri choncho, nchifukwa chiani Eva sanaime mpaka Adamu atamudziwa iye?

Zofanana . . . Funso lotsatira liri mwanjira yomweyo:

58. Kodi unali—mtengo weniwani umene Eva anadya chipatso chake? Iye anawona kuti iwo unali wabwino kuudya.

¹⁷⁸ Chabwino, m’bale, mlongo, yense yemwe anali, tiyeni tipite mmbuyo mu Genesis ndi ku kukapezamo chinachake apa. Tiyeni tipite ku Genesis 3:8, ngati inu mungatero. Chabwino, ndipo mumvetsere mwacheru kwenikweni tsopano.

¹⁷⁹ Tsopano ine ndiibweretsapo nkhaniyo. Zonse zinali zangwiwo ndi zoyera, kunali kopanda tchimo kapena kopanda choipitsidwa. Tsopano ine nditenga . . . lanu . . . funso loyamba ili poyamba. Mtengo mu moyo . . . pakati pa munda, pakati pa mtengo. *Mtengowo* unali “mkazi.” Tsopano ine nditsimikizira

izo kwa inu mwa Malemba ngati inu muti mungokhala opirira mu maminiti pang'ono.

180 Ife titenga moyamba ngati iye anali...ngati iye anaima Adamu asanamudziwe iye kapena ayi, kapena asan... Mvetserani:

Ndipo iwo anamva liwu la AMBUYE Mulungu akuyenda mmundawo, ndipo mu kachisisira ka tsiku: ndipo Adamu ndi mkazi wake anadzibisa iwo okha ku kukhalapo kwa AMBUYE Mulungu pakati pa mitengo ya mmunda.

Ndipo AMBUYE...anaitana kwa Adamu, ndipo anati...Kodi iwe uli kuti?

Ndipo iye anati, ine ndinamva mawu anu mmunda, ndipo ine ndimachita mantha, chifukwa ine ndinali maliseche;... (tsopano, iye sanali kuzidziwa izo dzana lake; chinachake chinali chitachitika, chinachake chinaululira kwa iye kuti iye anali maliseche)... ndipo ine ndinadzibisa ndekha.

Ndipo iye anati, Ndani anakuuza iwe kuti unali wamaliseche? Kodi iwe wadya za mtengo, ...?

181 Kudya za mtengo kumupangitsa iye kuzindikira kuti iye anali maliseche? Monga ine ndakhala ndikunena nthawizonse, (iyi si nthabwala ayi, ine sindikutanthauza kuti iyo ikhale nthabwala) “Koma ngati kudya maapulo kunawapangitsa akazi kuti azizindikira kuti ali maliseche ife kulibwino tipereke maapulo kachiwiri.” Mwaona? Iwo sunali umaliseche...Iwo sunali mtengo, apulo yomwe iwo anaidya, iko kunali kugonana. Penyani:

...Kodi iwe wadya za mtengo, umene Ine ndinakulamulira iwe kuti iwe usamaudye?

Ndipo mwamunayo anati, Mkazi yemwe inu munandipatsa ine kuti azikhala nane, iyeyo anandipatsa ine...mtengowo, ndipo ine ndinadya.

Ndipo AMBUYE...anati kwa mkaziyo, Ichi ndi chiani chomwe iwe wachichita? Ndipo mkaziyo anati, Serpenti anandinyenga ine, ... (nha?)...Serpenti anandinyenga ine, ndipo ine ndinadya. (nthawi yaitali iye asanaime, mwaona, ndi Adamu)

182 Adamu anamudziwa iye, ndipo iye anaima ndipo anabalapo—ndipo anabalapo Abele.

183 Koma ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu, basi kuchokera pa kuima kwenikweni. Tsopano kuti nditsimikizire kwa inu kuti mkaziyo anali mtengowo, mkazi aliyense ndi chipatso cha mtengo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Kodi inu sindinu chipatso cha amayi anu? Ndithudi, inu muli. “Ndipo pakati

pa chipatso, kapena pakati pa mtengowo, chipatso choti iye asamachikhudze.”

184 Ngati inu mungazindikire, kodi Yesu sanali Mtengo wa Moyo? Kodi Iye sanalonjeze mu Mateyu Woyera...kapena Yohane Woyera, mutu wa 6, “Ine ndine Mkate wa Moyo umene unachokera kwa Mulungu Kumwamba”?

185 Ngati munthu adya za mkazi...Ndipo yang’anani, kupyolera mu kubala kwa...mwa mkazi, ife tonse timafa; chifukwa ndife oti tidzafa (ndi kulondola uko?) kupyolera mu kubala kwa mkazi. Kupyolera mu kubala kwa mwamuna, ife tonse tidzakhala moyo kwanthawi zonse. Mkazi ndi mtengo wa imfa, mwamuna ndi mtengo wa moyo; pakuti mkazi samanyamula konse moyo mwa iye. Ndizo ndendende kulondola. N—nyongolosi ya moyo imachokera mwa mwamuna, molondola. Imapita mwa mkazi, ndipo mkazi si kanthu koma chofungatira; ndipo mwanayo samalumikizana naye, mchombo wokha. Palibe chidutswa chimodzi cha magazi a mayi omwe ali mwa mwanayo; amabadwira mu magazi ake, koma mulibe kachidutswa kamodzi *mwa* mwanayo. Pitani mukafufuze...kapena mukawerenge bukhu la adotolo, kapena mukawafunse adotolo anu, inu mukawona. Iwo mulibemo umo, ayi, bwana, mulibe kachidutswa kamodzi ka iwo konse. Iye wangokhala dzira chabe, ndizo zonse. Ndipo moyo umabwera kuchokera kwa mwamuna.

186 Ichu ndi choimira chokongola kuti zisonyeze kuti kupyolera mwa mkazi, kupyolera mu kubadwa kwachirengedwe, ife tonse tidzayenera kuti tidzafe, chifukwa ndife okufa pa kuyamba pomwe; ndipo kupyolera mwa Mwamuna Khristu Yesu yekha ife tingakhoze kukhala moyo. Ndipo apo pali mitengo iwiriyo mMunda wa Edeni. Kodi inu simukukhoza kuziwona izo?

187 Ndipo penyani! Ndipo mu tsiku limenelo panali Mkerubi anaikidwa kuti aziwulondera mtengo uwu. Kuti ngati iwo akanalawa konse za Mtengo wa Moyo uwo, iwo onse akanamakhala moyo kwa nthawi zonse. Ndi angati akudziwa zimenezo? Iwo onse akanamadzakhala moyo kwa nthawi zonse. Ndipo nthawi yoyamba iwo akanati awulawe iwo... Mngelo anati, “Ife tiziwulondera Iwo.” Ndipo anaika Akerubiwo pamenepo ndi malupanga amoto cha kummawa kuti aziwulondera Iwo. Iwo anawutengera Iwo kubwerera Kummawa, ndipo ankawulondera Mtengo umenewo ndi malupanga amoto chotero kuti iwo sakanakhoza kulowa umo nkukautenga Iwo (Mtengo uwu).

188 Ndipo pamene Yesu anabwera, Iye anati, “Ine ndine Mkate wa Moyo, kuti munthu akadya mkate uwu sadzafa konse.” Ndi uwo Mtengo wanu.

189 Ndi uyo mkazi wanu, ndi uko kugonana kwanu komwe kumabweretsa imfa. Motsimikiza basi monga pali chikhumbo chakugonana, pali imfa imasiyidwa nako. Ndipo motsimikiza

monga pali kubadwa kwauzimu, pali Moyo Wamuyaya umasiyidwa ndi Iwo. Imfa imabwera kupyolera mu kubadwira kwa mkazi, ndipo Moyo umabwera kupyolera mu kubadwira kwa Mwamuna. Ameni! Ndi inu apo.

¹⁹⁰ Tsopano tiyeni tizitengere mmbuyo kwa Kaini. Kodi inu mungandiuze ine kumene mzimu uwo ndi nkhanza iyo inachokera? Ngati Kaini...penyani, ngati Kaini anali mwana wa Adamu yemwe anali mwana wa Mulungu, kodi choipa icho chinachokera kuti? Chinthu choyamba pamene iye anabadwa, iye ankamuda wina, iye anali wakupha, iye anali wansanje. Ndipo tsopano tengani chikhaliidwe cha abambo ake, koyambirira komwe ku chiyambi, Lusifara, ndipo iye anali pa chiyambi...iye anali kuchita nsanje ndi Mikaeli, chomwe chinayambitsa vuto lonseli. Ndi angati akuzidziwa izo? Ndipo Kaini anali wa chikhaliidwe cha bambo wake, chomwe iye anamuchitira nsanje m'bale wake ndipo anamupha iye. Wangwiro uyo...chikhaliidwe icho sichikanakhoza kubwera kuchokera kwa msempha wangwiro uja. Icho chinabwera... chinkayenera kuti chibwere kudzera mu msempha wopotozedwa uwu. Ndipo zindikirani Kaini, mwamsanga pamene iye anabadwa.

¹⁹¹ Ndiyeno Abele anabadwa pambuyo pa iye, ndiye iye anaima ndi Adamu, ndipo iye anadziwa—anamudziwa iye ndipo iye anabala mwana Abele. Ndipo Abele anali choimira cha Khristu; ndipo pa—pamene Abele anaphedwa, Seti anadzatenga malo ake; imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Khristu, mu choimira.

¹⁹² Koma, tsopano, Kaini ankapembedza; ntchito zake zonse zachithupithupi, basi monga mpingo wa chithupithupi lero: iwo amapita ku tchalitchi, iwo amapembedza, Kaini ankapembedza; iye sanali wachikunja, iye sanali wa chikominisi. Kaini anali wokhulupirira; iye anapita kwa Mulungu, iye anamanga guwa. Iye anachita chinthu chachipembedzo chirichonse chimene Abele anachita, koma iye analibe vumbulutso lauzimu la chifuniro cha Mulungu. Lodala likhale Dzina la Ambuye! Ndi inu apo. Kodi inu mukuziwona Izo? Iye analibe vumbulutso lauzimu, ndipo ndilo vuto ndi mpingo lero. Ndipo Yesu anati Iye akanadzamanga Mpingo Wake pa vumbulutso lauzimu ilo. Inu mukumvetsa Izo? O, mai, maso anu akhoza kutseguka tsopano. Mwaona, vumbulutso lauzimu.

¹⁹³ Kaini anabwera: iye anamanga guwa, iye anapembedza, iye anabweretsa nsembe, iye anagwada pansu, iye anamutamanda Mulungu, iye anamupembedza Mulungu, iye anachita chirichonse chachipembedzo chimene Abele anachita. Ndipo Mulungu mwapoyera anamukana iye chifukwa iye analibe vumbulutso lauzimu!

194 Utsatireni mzere womwewo wa Kaini: chotsika kumene mpaka ku chombo, kuchokera ku chombo mpaka kwa Israeli, kuchokera kwa Israeli mpaka kwa Yesu, ndipo kuchokera kwa Yesu mpakana ku tsiku lino; ndipo muwone ngati mpingo wachithupithupi uwo, wachikhazikitso, wouma ndi wokhuthara, wausikolala, ine ndikutanthauza mwamuna yemwe ali ndi malemba, yemwe amadziwa chiphunzitso chonse ndi mafioloje, iwo akhoza kuzifotokoza izo, mnyamata, basi monga [M'bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi.] choncho, koma opanda vumbulutso lauzimu! Ndiko kulondola. Ndicho chiphunzitso cha Kaini.

195 Baibulo linati, “Tsoka kwa iwo! chifukwa iwo anapita mu chiphunzitso cha Kaini, anathamanga mwa kulakwitsa kwa Balaamu, ndipo anawonongeka mu kalankhulidwe kokopa ka Kora.” Bukhu lomwelo, Yuda, iye anati, “Iwo anakonzedweratu ku chiwonongeko ichi.” Ndithudi, iwo ali. Mwaona? Kodi Balaamu anali chiani? Iye anali bishopu. Iye anali woyang’anira zonse wa mpingo. Iye anabwera apo mwachikhazikitso basi monga iye akanakhallira. Iye anapereka . . . Tayang’anani pa iye ataima apo moyamikirika, ataima apo moyamikirika kwambiri. Ndipo iwo sanali achikunja, iwo anali okhulupirira.

196 F—fuko lija la Moabu linachokera kwa mwanawamkazi wa Loti. Loti yemwe anakhala . . . Mwana wamkazi wa Loti yemwe anagonana ndi abambo ake, ndipo anaima ndipo anabala mwana, ndipo mwana ameneyo anali . . . anaphukitsa mtundu wa Moabu. Ndipo iwo anali chipembedzo chachikulu. Anthu aakulu, azosangalatsa, ndipo iwo anali nawo afumukazi ndi mafumu ndi oyamikirika. Iwo anali ndi mabishopu ndi makadinolo ndi chirichonse.

197 Ndipo apa panabwera gulu la oyera odzigudubuza, gulu linalo, Israeli; gulu laling’ono lachikale lomwe silinali mwachipembedzo, zipembedzo zosakanizikana. Ndipo iwo ankachita chirichonse chomwe chinalipo pa mapu kuti chichitidwe, zoipa nazonso. Koma chomwe izo zinali, iwo anali nalo vumbulutso lauzimu, ndipo Mulungu anali ndi iwo mu Lawi la Moto.

198 O, i—ine ndikudziwa iwo anali nazo zinthu zachithupithupi, ndipo anthu ankati, “Gulu lotero la zamngalande monga izo, palibe chomwe akanachita koma kuwathamangitsako iwo.” Koma iwo anali nalo vumbulutso lauzimu, ndipo iwo anali nalo Thanthe lokanthidwa, iwo anali nayo njoka ya mkuwa, iwo anali nalo Lawi la Moyo likupita limodzi nao. Aleluya! Ine ndikudziwa i—inu mukuganiza kuti ine ndatentheka, koma ine sindiri. Ine ndikungomverera bwino.

199 Zindikirani! Pamene ine ndikuganiza, “Mulungu uyo yemwe, lero, akukhala ndi ife.” Ilo likadali vumbulutso lauzimu

la Mawu. Ndithudi, ilo liri. Ndi zolondola Mwamuyaya. Lodala likhale Dzina la Ambuye! Inde, bwana.

²⁰⁰ Apa anaima iye pamwamba apo, ndi gulu lachikhazikitso; gulu la Abaptisti ndi Apresbateria ataima pa phiri, ndipo anamutengera bishopu wawo kumeneko. Ndipo iwo anali basi achipembedzo, ndi mtundu womwewo wa chipembedzo, iwo ankamupembedza Mulungu yemweyo. Iwo anati, “Tayang’anani pansu apo pa gulu ilo la zinyalala. Bwanji, iwo alibe ngakhale chipembedzo. Iwo si kanthu koma gulu lonjenjemera, kukuwa, oyera odzigudubuza.”

²⁰¹ Ndi kulondola uko? Ndendende, iwo anali. Ngati inu simukukhulupirira kuti iwo anali oyera odzigudubuza, bwererani mu Genesis ndi kukapeza izo pamene iwo ankawoloka. Ndipo chozizwitsa chitachitidwa, ndipo Miriamu anatenga nkhotcho ndipo anatsika ndi gombe, akuiwomba iyo; akuvina mu Mzimu, ndipo Mose anaimba mu Mzimu. Ngati ilo si gulu lomwe ife tinalitcha omasuka . . . oyera odzigudubuza, ine sindikudziwa chomwe ilo liri; akuimba ndi kumalumpha ndi kumatamanda. Ndipo nthawi yonse mafuko ankawada iwo, koma Mulungu anali ndi iwo. Iwo anali nalo vumbulutso lauzimu, anali akulitsatira Lawi la Moto.

²⁰² Ndipo Moabu anati, “Tsopano, tapenyani apa. Ife tiwaitana makadinolo onse ndi mabishopu onse, ndi akulu akulu onse, ndipo tiwabweretsa iwo kuno. Ife tichita chinachake ndi icho, chifukwa ndife fuko lachipembedzo. Ife sitilola kuti kudzifalitsa uko tisikanizikane nako mu chipembedzo chathu chabwinochi.”

²⁰³ Ndipo kotero iwo anawabweretsa iwo kumeneko. Ndipo iwo anamanga maguwa thwelofu; ndizo basi ndendende zomwe Israeli anali nazo, maguwa thwelofu. Iwo anaika nsembe thwelofu pa iwo, ng’ombe; ndendende basi zomwe Israeli anali nazo, zomwe Mulungu ankafuna. Iwo anaika nkhusa thwelofu pa iwo, kuimira kudza kwa Ambuye Yesu Khristu; nkhusa thwelofu mu malo onsewo.

²⁰⁴ Oyamikirika onse, mabishopu ndi onse, anaima mozungulira. Iwo anayatsa nsembezo. Iwo anapemphera, iwo anakwezera manja awo kwa Yehova ndipo anati, “Yehova, timveni ife!” Kodi iwo anali kuyesera kuchita chiani? Ndipo Balaamu wawo wachikulireyo anapita uko monga choncho, ndipo Mzimu unatsikira pa iye. Zedi (koma iye anali wachithupithupi).

²⁰⁵ Mzimu ukhoza kugwera pa wachinyengo, Baibulo linatero. Inu munandimva ine ndikuphunzitsa izo, tsopano. “Mvula imagwera pa wolungama ndi wosalungama.” Koma izo zinkayenera kuti zizifanana ndi Mawu, apo ndi pamene inu mumazipeza izo.

206 Ndiye pamene iye anatero, ndipo...pamene Mzimu, ngakhale, uli pa iye unkanena Choonadi, iye anayesera kuti amutemberere Israeli, ndipo Iye ankamudalitsa Israeli.

207 Tsopano, ngati Mulungu amangolemekeza mpingo wabwino, ndi bishopu wabwino, ndi m'busa wodabwitsa, gulu la anthu ausikolala, Iye anali wokakamizika kuti ayilandire nsembe imeneyo, chifukwa iye anali basi wolondola mwachikhazikitso monga Israeli anali wolondola; koma iye analibe vumbulutso lauzimu la Mawu ndi chifuniro cha Mulungu. Ndi inu apo, ndiko kusiyana kwake lero.

208 Tayang'anani pa Yesu. Iwo anati, "Kutali naye munthu ameneyo. Ife tikudziwa iye ndi Msamaria. Iye ndi wopenga. Kodi iwe ungatiphunzitse ife? Pakuti, iwe unabadwa mu chigololo. Iwe sunali kanthu koma mwana wapathengo woti uzibwera naye. Bambo ako ndi ndani? Ukuti Mulungu ndi bambo ako, iwe wochitira mwano! Bwanji, iwe ukutanthauza kuti iwe ife? Ife takhala tiri alaliki, ife takhala tiri bishopu; kudzera mwa agogo-agogo-agogo-agogo-agogo-agogo-agogo-agogo-aamuna anali alaliki ndi bishopu. Ife tinabadwa ndi kuleredwa mu mpingo. Ife takhala tikudutsa mu maseminare apamwamba mwamba. Ife timawadziwa Mawu aliwone ku chilembo. Ndipo iwe ukuyesera kuti utiphunzitse ife? Nkuti komwe iwe unayambapo wapita ku sukulu? Nkuti komwe iwe unakapeza kuphunzira uku?"

209 Iye anati, "Ndinu a . . . atate anu Mdierekezi," anatero Yesu.

210 Iwo analibe zizindikiro ndi zodabwitsa pakati pawo. Iwo analibe machiritso Auzimu ndi zinthu pakati pa iwo. Iwo analibe madalitso pakati pa iwo. Koma Yesu anali mwamtheradi vumbulutso lauzimu la Malemba.

211 Iwo anati, "Bwanji, izo zinalembedwa *mwakuti-n-mwakuti*."

212 Ndipo Yesu anati, "Inde, ndiponso kunalembedwa." Koma Mulungu anamuzindikiritsa munthu Wake ndi zizindikiro zake.

213 Petro ananena mofanana, pa Machitidwe 2, iye anati, "Inu amuna amu Israeli; Yesu waku Nazareti, mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati pa inu, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zomwe Mulungu ankachita ndi Iye pakati pathu, ndi zomwe inu nonse eniake mukuzidziwa." (ndi inu apo) "Iye pokhala atawomboledwa n...n kud-...ndi Gulu lalikulu la Sanhedrin cha uko. Koma mwakudziwidwiratu kwa Mulungu, Mulungu atamudzozeratu Iye kuti adzafe imfa iyi. Inu munamupereka Iye ndi manja ankhaza ndi oyipa. Inu munamupachika Kalonga wa Moyo, Yemwe Mulungu anamuwukitsa. Ndipo ndife mboni za izo."

214 Psfyuu, mlaliki wakeyo! Sanali . . . iye sankakhoza ngakhale kulemba dzina lake lomwe, koma iye ankamudziwa Mulungu.

Iwo anati iwo “anamvetsera kwa iye kuti anakhala ali ndi Yesu.” Ndithudi, ndi vumbulutso lauzimu. O, mai. Tsopano, ndi inu apo.

²¹⁵ Kaini anali basi mu mzere umenewo, mpingo wa chithupithupi uwo uli mu mzere womwewo lero. Mpingo Wauzimu ukadali nalobe Lawi la Moto, ukadali nazobe zizindikiro, zodabwitsa, ukadali naye Khristu yemweyo; zomwe zimatsimikiziritsa njira yonse kuchokera kwa mwanawankhosa wakufa, ndi mMunda wa Edeni, mpaka kudza kwachiwiri kwa Mwanawankhosa. Mwamtheradi, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

²¹⁶ Ndipo mzere uwo wa Kaini, wachipembedzo ndi wopukutidwa ndi wausikolala, chotsika pansi chimodzimidzi; mofanana basi, tsiku lililonse chimodzimidzi basi. Otsutsa ndi ozunza, monga Kaini anali kwa Abele, mmomwenso iwo ali lero, ndipo akhala ali ndipo nthawizonse adzakhala ali; achithupithupi, osakhulupirira. Ndiko kulondola.

²¹⁷ Tsopano Genesis 3:8, ndiponso ine ndinaika 20 apa, ine ndinali kuziyang’ana kanthawi kapitako:

Ndipo Adamu anamutcha...Ndipo Adamu anamutcha mkazi wake...Eva; chifukwa iye anali mayi wa amoyo onse. (mwaona, izo zinali pambuyo pa kunyenga uku kutachitika kale)

²¹⁸ Kaini anali... “Tsopano dikirani!” Inu mukuti, “Ikanakhoza bwanji njoka, serpenti?”

²¹⁹ Koma, m’bale, penyani apa, Baibulo silimanena kuti iye anali serpenti; Baibulo linati, “Iye anali chochenjera kwambiri mwa zinyama zonse za mmunda.” Iye sanali chokwawa ndi mimba, iye anali chirombo. Iye anali... Ndipo apo... .

²²⁰ Ndipo mudirole ine ndingokupatsani inu ichi ngati chizindikiro pang’ono pakati pa ife, ngati inu mungathe. Apo ndi pamene sayansi imasokoneza yonse. Chinthu chapafupi chimene iwo angakhoze kuchipeza kwa munthu, ndi chimpazi. Ndi angati akudziwa zimenezo? Koma pali chinachake pakati apo. Iwo sangakhoze kuwapanga mafupa a chimpanzi kukomana ndi mafupa a munthu, komabe ndi chinthu chapafupi kwambiri. Iwo akhoza kumubweretsa iye kuchokera kwa mbululu. Iwo akhoza kumubweretsa iye kuchokera kwa namchidwe. Iwo akhoza kumubweretsa iye kwa chinyama ndi chinyama chirichonse. Iwo akhoza kumubweretsa iye kwa chimbalangondo. Inu muchitenge chimbalangondo ndi kuchisenda chikopa pa icho, chimangokhala ngati mkazi wamng’ono. Basi chinthu chofanana. Mutengereni iye mmbuyo ndi chirichonse, mukaziimitse izo apo, ndi kupita uko kukamukoka mkazi monga...kumuimika mkaziyo monga choncho. Zimangokhala chimodzimidzi basi ngati—ngati chimbalangondo. Phazi limayenda chimodzimidzi, ndipo dzanja

limayenda monga chonchi, chimodzimodzi ngati munthu. Koma chimpazi chimayandira kuposa izo. Ndi za pafupifupi, koma iwo sangakhoze kuchipeza icho.

²²¹ Pano pali chinsinsi chaching’ono, ngati inu mukufuna kuti muchidziwe icho. Inu mukudziwa komwe izo ziri? Izo zinabisika kwa iwo. Iwo akhoza kufukula mafupa onse omwe iwo akuwafuna. Iwo akhoza kufukula. . . Osema akhoza kufukula, ndi asayansi, n—ndipo azamakedzana akhoza kuyesa zopimira za nthawi ndi miyezo ya atomiki, koma iwo sadzakhoza konse kuzigwira izo. Pakuti uyo anali serpenti yemwe anali mochuluka kwambiri ngati munthu kuposa chirichonse chomwe chinalipo padziko lapansi, ndipo Mulungu anamutemberera iye ndipo anamuika iye pa mimba yake, ndipo iye wabwerera kukakhala njoka ndipo alibe nkomwe kufanana ndi munthu. Tsopano ingokandani mutu wanu, asayansi awo, ndipo muwalole iwo atenge izo kwa kanthawi.

²²² Koma Baibulo limanena kuti, “Iye anali wochenjera kwambiri mwa zamoyo zonse za kuthengo.” Ndiko kulondola. Iye anali chilumikizano icho chomwe chikuima pakati pa munthu ndi nyani, ndipo Mulungu anamutemberera iye ndipo anamuika iye kubwerera pa mimba yake chifukwa c—cha chinthu chomwe iye anachita. Iye anamunyenga mkazi uyu, ndipo anabala mwana wake woyamba yemwe anali Kaini, wa chikhalidwe cha serpenti, cha kudzoza chake, Mdierekezi, yemwe analowa mwa serpenti, nyemwe anachita izo.

²²³ Ndiyeno iye anaima ndipo anabala, iye anaima kachiwiri iye atatha kunyengedwa. Tsopano penyani, iye ananyenga, iye anali pafupifupi. . . Chabwino, iye anachita cholakwika. Koma iye, kwenikweni, anali movomerezeka pamene iye anaima ndi mwamuna wake, pakuti izo ziyenera kuti zinali, nthawi zambirimbiri mtsogolo mwake, miyezi yambiri ndi masiku ambiri mtsogolo mwake; inu simungakhoze kudziwa izo, ife sitikudziwa, koma iye anabala Adamu.

²²⁴ Ndipo winawake anapeza funso, anati, “Chabwino, mwana. . . iye anati iye anali akupita. . . Monga Kaini anabadwa, anati iye ‘analandira mwana kwa Ambuye.’” Mwamtheradi, ndithudi, izo zinkayenera kukhala ziri. Ilo linali lamulo la chilengedwe. Ndizo ndendende basi momwe inu muliri lero. Pamene inu mubadwa kachiwiri, Mulungu samangobwera pansu ndi kudzakupangani inu. Ndinu mphukira ya atate anu ndi amanu. Ndipo inu mudzakhala. . . padzakhala. . . ana anu adzakhala mphukira za inu. Ndi kubalana nthawi zonse, mpaka pansu, monga mbewu za mitengo ndi zinthu monga choncho; koma kubwerera ku chapachiyambi. Ine ndikuyembekeza izo zikufotokoza izo.

²²⁵ Kodi tiri nayo nthawi yochuluka bwanji? Tiribe ena moonjezera. Mvetserani kwa lina labwino lotsatira ili. . . lomwe

ife tidzalitenge Lamlungu: “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi...” (Ife tikufuna kuti tidziwe izo.) “...Khristu.” Pa nthawi...Tsopano, ine ndikuganiza ine nditenga malemba ena, malemba abwino pa izo [M’bale Branham akuyankha ili mu Gawo 11, paragrafu 361, ngati funso 60—Mkonzi.]

²²⁶ Pano pali lina labwino, chimodzimodzi ngati...Kodi inu mungandilole ine miniti ina imodzi kapena awiri, kuti ndiyankhe ili? Ilo likhoza kudziyankha lokha.

59. Pamene—pamene inu mukuti “oyipa sadzawotchedwa Kwamuyaya,”... (Chabwino, tsopano ine ndiri nawo Amboni za Yehova akuthamangira apo, sichoncho ine?)... Pamene inu mukuti oyipa sadzawotchedwa Kwamuyaya, kodi inu mukutanthauza mu hade kapena mu nyanja ya moto? Ine ndikudziwa amanena mu Chivumbulutso (ndiwo mutu wa 20) kuti gehena adzaponyedwa mu nyanja ya moto. Ngati iwo sadzawotchedwa Kwamuyaya, ndiye chidzachtike ndi chiani ndi iwo?

²²⁷ Basi monga ine ndangotsirizira kunena, m’bale kapena mlongo, yense yemwe anali; iwo adzatheratu osawonekanso, sikudzakhalanso kanthu kwa iwo. Iwo anali nacho chiyambi, ndipo apo iwo akutha; iwo sali basi kanthu kenanso. Adzatan...adzawotchedwa motalika chotani, izo nzovuta kunena. Koma, penyani, apo...

²²⁸ Ngati inu mungakhoze kungotengera izi mu malingaliro anu, onani, ndi zophweka kwambiri. Ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo iwo umabwera kudzera mwa Mulungu Mwiniwake. Ndipo Mulungu yekha ndiye Moyo Wamuyaya. Ngati inu mungati mungofika umu mu lexicon, muyang’ane pa mawu Achigiriki *Zoe*. *Zoe* ndi “Moyo Wamuyaya.” *Moyo Wamuyaya* ndi “Mulungu.” Ndipo Yesu anati, “Ine ndipereka kwa iwo Moyo Wamuyaya.” Ndipo ngati inu mungayang’ane umu mu lexicon, ilo linati, “*Zoe*.” Ndiwo Moyo Wamuyaya wokha umene ulipo. Palibe malo mu Baibulo pomwe Ilo limati padzakhala Gehena Wamuyaya, ilo limati iwo adzawotchedwa “kwanthawi zanthawi.”

²²⁹ Tsopano, kuti mutenge mawu okuti “kwanthawi zanthawi.” Yang’anani pa *aeon—aeon*. Kodi inu munazindikira apa mu Baibulo? Ndi angati anayamba amvapo izo zikunenedwa, “Ndipo ma *aeon* ndi ae—...”? Ndi angati akudziwa kuti *aeon* ndi “danga la nthawi”? Bwanji, zedi, aliyense akudziwa kuti *aeon* ndi “danga la nthawi.”

²³⁰ “Ndipo iwo adzawotchedwa kwa ma *aeon*,” ndiwo madanga a nthawi. “Adzaponyedwera mu nyanja ya moto, ndipo adzapsya kwa ma *aeon*.” *Ma aeon* amatanthauza “madanga a nthawi.” Iwo akhoza kudzawotchedwa kwa zaka mazana milioni mu chilango koma, potsiriza, iwo adzayenera kuti

adzabwere ku mathero; kuti asadzawonekenso, palimodzi. Mwaona, chifukwa chirichonse chomwe sichiri changwirowo ndi chopotozedwa kuchokera ku Changwirowo; ndipo icho chinali ndi chiyambi, kotero icho chiyenera kukhala ndi mathero.

²³¹ Koma ife amene timakhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu tiri ndi Zoe, “Moyo womwe wa Mulungu” mwa ife, ndipo tiri nawo Moyo Wamuyaya. Osati tiri ndi moyo wanthawi zanthawi, wochimwa ali nawo moyo wa nthawi zanthawi, koma ife tiri nawo “Moyo Wamuyaya.”

²³² M'bale Cox, osati kale litali, anali atakhala pa kanjira kanga ife tisanaike. . . titatha kuika miyala pamenepo, ndipo iye anatola chaching'ono, choumbidwira mmwala, ndipo iye anati, “M'bale Branham, chakhalamo utali wanji chimenecho?”

²³³ “O,” ine ndinati, “mwazaka, inu mukhoza kunena kuti chakhalamo kwa zaka makumi khumi. Mtundu wina wa chirombo chaching'ono, chakale cha mmadzi chomwe chinakhala nthawi ina, kanyama kakang'ono ka mmadzi, mwina kanakhala mmbuyomo mu mibadwo inapitayo.”

²³⁴ Iye anati, “Tangoganizani momwe moyo wa munthu uliri waufupi kwa moyo *uwo*.”

²³⁵ Ine ndinati, “O, koma, m'bale, chinthu icho chiri nawo mathero, koma Moyo umene ife tiri nawo mwa Khristu ulibe mathero. Icho chikhoza kukhala moyo *nthawizonse* ziwiri kapena zitatu, koma icho sichidzakhala nawo konse Moyo Wamuyaya, chifukwa Moyo Wamuyaya umabwera kuchokera kwa Mulungu yekha.”

²³⁶ Wamuyaya, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo sadzabwera KONSE ku chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Ndi inu apo, inu mumakhala nawo Moyo Wamuyaya pakukhala wokhulupirira. Wosakhulupirira amakhala ndi moyo wa nthawi zonse. Wamuyaya. . . wokhulupirira amakhala ndi Moyo Wamuyaya, ndipo sangakhoze kuwonongeka chifukwa Iye ndi Wamuyaya.

²³⁷ Koma wokhulupirira, iye adzapita. . . Wosakhulupirira adzadutsa mdziko, iye adzakhala nazo zisoni, ndi matsoka; zomwe iye amadzitcha kukhala ndi nthawi yaikulu, “whupii, akukhala ndi nthawi yaikulu.” Akazi, vinyo, ndi nthawi yaikulu, iye amaganiza kuti iye akupitirira. Iye adzafa, iye adzapita mu nyanja yamoto ndi miyala ya moto yomwe imayaka, komwe kuyaka kukuchitika mopitirira kwanthawi za nthawi, ndipo mwinamwake kwa zaka ma milioni mazana solo yake ingati idzazunzidwe mu nyanja ya moto ndi mwala wamoto.

²³⁸ Ine. . . Inu mukuti, “Kodi iyo idzangokhala ngati miyala ya moto yachizolowezi?” Ine ndikukhulupirira iyo idzakhala kuchulukitsa kamilioni kuipa kwake kuposa apo. Ine

ndikukhulupirira inu simungakhoze kuzifotokoza izo ndi moto, ndi moto weniweniwu. Chifukwa chokha izo akuti “mwa moto,” moto uwo ndi chinthu chonyeketsa kwambiri chomwe ife tiri nacho. Iwo mwamtheradi umanyeketsa ndi kuwononga chirichonse, moto umatero. Chabwino, ndiye, zidzakhala ziri mmenemo, koma inu mudzakhala nayo solo yomwe iti idzachite kulangidwa kupyolera mu mtundu winawake wa . . .

²³⁹ Tsopano, inu muyenera kuti muwapenye mawu oti *moto*, chifukwa Mzimu Woyera ukugwiritsidwa ntchito “Mzimu Woyera ndi moto”; chifukwa moto wa Mzimu Woyera amawotcha tchimo nkulichotsa, mwaona, ndipo umapangitsa kuti chiyere.

²⁴⁰ Koma moto *uwu*, iwo ukuchokera ku gehena, ilo linati “nyanja ya moto.” Ndipo chirichonse chomwe iwo uli, ndi chilango cha kuzunza. Bambo wolemara anakweza maso ake, ali mu gehena, ndipo anati, “Mutumizeni Lazaro ndi madzi pang’ono a pa zala zake, kuti ndiike pa milomo yanga, pakuti malawi awa akundizunza ine.” Musati muziganiza kuti kulibe gehena yoyaka, ndipo gehena yeniyeni, uko ilipo. Ngati kuli Mdierekezi weniweni, kuli gehena yeniyeni.

²⁴¹ Koma, inu mukuona, chirichonse chomwe chiri chopotozedwa chiri ndi mapeto kwa icho, chifukwa icho potsiriza chiyenera kudzabwerera ku ungwiro uwo ndi chihero cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Wamuyaya; ndipo ngati ife tiri nawo Moyo Wamuyaya, Mulungu ali mwa ife, ndipo ife sitingakhosenso kufa monganso Mulungu sangakhoze kufa. Ndi inu apo.

²⁴² Tsopano, nkhanayi ndithudi ikudzifotokoza Yokha, mwaona, ndipo ikupangitsa izo kukhala zolondola. Tsopano, tiyeni tiwone, ine ndinali . . . ine sindikudziwa ngati . . . Inde:

“Nchiani chiti—chidzachitika nchiani kwa iwo?”

²⁴³ Iwo adzatheratu, palibe chinanso kwa iwo: solo idzapita, mzimu udzapita, moyo udzapita, thupi lidzapita, malingaliro adzapita, kukumbukira kudzapita.

²⁴⁴ Ndipo sikudzakhala kulinso ngakhale malingaliro oyipa, kapena ngakhale izo—ngakhale zikanadzachitikapo, mu Ulemerero. Ndiko kulondola, izo zonse zidzakhala . . . Kodi inu mungalingalire, kuti kuno kudzakhala kuli anthu cha kuno mu gawo ili . . .

²⁴⁵ Kodi Baibulo silimati, “Ngakhale malingaliro a oyipa adzawonongedwa”? Malingaliro omwe a iwo adzawonongedwa.

²⁴⁶ Apa padzakhala pali munthu cha *apa*, apa pali Mulungu Wamkulu Woyera Uyo *apa*, ndipo podziwa kuti kutali uko komwe kuli dzenje liri ndi solo ikuwotchedwa mmenemo? Bwanji, uko sikukanakhoza kukhala Kumwamba. Malingaliro, omwe, zokumbukira zomwe, chirichonse chomwe

chiri chopotozedwa, lingaliro loipa lirilonse, chirichonse chidzawonongeka, ndi chirichonse chomwe chiri choipa mwa icho. Ndipo ife sitidzakhala kanthu koma ungwiro, ndi Zoe, Moyo wa Mulungu; ku Muyaya, ndipo kwa mibadwo ikugudubuzika, mopitirira, pitirira, ndi kupitirira, pitirira; Izo sizidzatha konse, zikhala Zamuyaya!

247 “Iwo anapita mu chilango *chosatha*, koma olungama anapita mu Moyo Wamuyaya.” Inu mukuzimvetsa izo? Chilango *chosatha*, Moyo Wamuyaya, kusiyana kwakeko.

248 Tsopano, onani, izo siziti. . . Tsopano, ine ndikudziwa, kwa inu, ang’ono okonedwa anga, i—ine sindikutanthauza kuyesera kuti ndidzipereke ndekha ngati wodziwa zonse. Ngati ine ndichita izo. . .

249 Tsopano, ine ndiri nawo mafunso atatu kapena anai ena abwino. Ine ndidzawatenga iwo Lamlungu mmawa, Ambuye akalola.

250 Tsopano, taonani. Mwaona, izi zimautsa mafunso. Ndine mlaliki wachikulire. I—i—i—ine ndiri ndi zaka twente sikisi mu utumiki. Ndipo i—ine ndiri woyamikira kwambiri chifukwa cha izi, kuti ine ndikhoza kunena izi, zanga. . . ine sindinayambe ndayesera kuyesera kupereka chirichonse mu moyo wanga popanda poyamba icho kukhala chitaululidwa. Ndipo ndine wothokoza kwambiri kuti Mngelo wa Ambuye. . . Chimene ine ndinalibe maphunziro, ndinalibe kukhoza. Ndipo Mngelo uyu anatsika, ndipo wakhala ali thandizo langa lotumizidwa kuchokera kwa Mulungu. Ndipo Iye sanayambe wandiuzapo ine chinthu chimodzi koma chimene mwamtheradi chinkagwirizana kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso ndi icho, mochuluka chotero. . . ine ndinalimba apo mofulumira ndithu pamene Iye anati “Ndipo iwe—ndipo iwe udzatenga mphatso machiritso Auzimu.” Ndipo ine ndikuzinena izo basi momwe Iye ananenera izo.

251 Ndipo mu pafupi zaka zitatu mtsogolo mwake, manenjala anaitanitsa changa—tcheru changa kwa izo, anati, “M’bale Branham, kodi inu munazizindikira izo? Izo ndi zangwiro kwambiri mpaka Iye ngakhale anakuuzani inu kuti ‘kamphatso.’”

252 Mwaona, sanati konse “mphatso.” Ndipo aliyense—wina aliyense mu Baibulo. . . mphatso iliyonse ndi “kamphatso” koma machiritso Auzimu, ndipo ndi “mphatso.” Ndi “mphatso za machiritso.” Inu mukhoza kukhala nayo mitundu yonse ya mphatso za machiritso, mnjira zosiyana. Koma imodzi iliyonse ndi “mphatso”; “m” mphatso ya kunenera, “m” mphatso ya *ichi*. Koma machiritso Auzimu ali mu zambiri: “mphatso.” Ndipo ine sindinali nditazizindikira konse izo, kuti Mzimu Woyera ndi wangwiro kwambiri. O, adalitsike Ambuye!

253 Kodi inu mukumvetsa kuti Mzimu Woyera womwewo umene unalilemba Baibulo ilo, ndi mazana a anthu, mazana a zaka motalikirana. . . ndipo palibe mmodzi wa iwo anasiyana wina kwa mzake, aliyense wa iwo anali mwathunthu; ndipo wina asanamvepo konse za winayo.

254 Ndipo Paulo anapita uko, ndipo anali uko mu Arabia, ndipo sanakacheze konse ku Yerusalemu kwa zaka fortini, koma anali uko mu Yerusalemu ndi uko. . . anapita kuchokera. . . sanapite konse ku Yerusalemu. Koma anali ku Arabia, ndipo anayamba kulalikira, asanamuwone konse Petro ndi ena onse a iwo kwa zaka fortini. Ndipo pamene iwo anabwera palimodzi, iwo anali akulalikira chinthu chofanana kumene: ubatizo wa madzi mu Dzina la Yesu Khristu, ndi machiritso Auzimu, ndi mphamvu ya Mulungu.

255 O! Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao:

Mmodzi wao, mmodzi wao,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao; (aleluya)
Mmodzi wao, mmodzi wao,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao.

Kuli anthu kulikonse,
Mitima ikuyaka,
Ndi moto wa pa Pentekoste,
Wawatsuka nuwayeretsa;
Ukuyakano mu mtima mwanga,
Ulemerero kwa Dzinalo!
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao.

Anasonkhana pamwamba,
Akupemphera mu Dzina,
Nabatizidwa ndi Mzimu,
Mphamvu yautumiki nidza;
Chomwe anawachitira apo
Achitanso chomwecho,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao.

Mmodzi wao, mmodzi wao,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao; (aleluya)
Mmodzi wao, mmodzi wao,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao.

256 Mvetserani, ine ndiri ndi uthenga waung'ono kwa inu:

Bwera, m'bale, funa dalitso
Likuyeretsa ku tchimo,
Liyambitsa mabelu achimwemwe
Liyatsa moyo wako;
Likuyaka mu mtima wanga,
Ulemerero kwa Dzinalo,
Ndakondwa kuti ndine mmodzi wao.

257 Kodi sindinu okondwa kuti ndinu mmodzi wao? Ndi chiani icho? Ndi Mzimu umene umawulula. Ndi vumbulutso la Mulungu, “Pa thanthwe ili.” Ine sindikusamala ngati arkibishopu. . .

258 Wansembe wa Chikatolika anali atakhala, osati kale litali, mu nyumba yanga. Ndipo iye anati, “Bambo Branham, ine ndabwera kudzakufunsani inu funso.”

Ine ndinati, “Chabwino, bwana.”

Anati, “Ine ndiri ndi kalata pano yochokera kwa abishopu, ya kwa inu.”

Ine ndinati, “Chabwino, bwana.”

259 Iye anati, “Maneno omwe inu mumawapanga, kodi inu mungakweze dzanja lanu ndi kulumbira motsimikiza kuti inu mumanena zoonadi?”

260 Ine ndinati, “Ine sindingatero.” Ine ndinati, “Baibulo linati, ‘Musamalumbire konse, ndi miyamba kapena ndi dziko lapansi (pakuti ndi poponda mapazi Pake). Lolani inde wanu azikhala ayi ndi inde.’ Ngati abishopu akufuna kuti amve zomwe ine ndingati ndinene, iwo ayenera kutenga mawu anga pa izo. Ngati iwo satero, ine sindilumbira.”

261 Wansembe wamng’ono uyu kumtunda uko ku mpingo wa Mtima Woyera, iye anati, “Kodi inu munamubatiza Pauline Frazier pa tsiku *lakuti-lakuti*?”

262 Ine ndinati, “Ine ndinatero, bwana, uko mu Mtsinje wa Ohio.”

263 Anati, “Inu munamubatiza chotani iye?”

264 Ine ndinati, “Ine ndinamubatiza iye pa kumumiza iye pansu pa madzi mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.”

265 Iye anazilemba izo apo. Nati, “Inu mukudziwa, mpingo wa Katolika unkabatiza kalelo monga choncho.”

Ine ndinati, “Liti?”

Iye anati, “Mu m’badwo woyambirira.”

Ine ndinati, “M’badwo woyambirira wake uti?”

Iye anati, “Chabwino, pa chiyambi.”

Ine ndinati, “Chiyambi chake chiti?”

Iye anati, “Mu Baibulo.”

Ine ndinati, “Kodi inu mukutanthauza koya-. . .m—mwa ophunzira?”

Iye anati, “Ndithudi.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumawatcha Akatolika a. . .Inu mukuti ophunzirawo anali Akatolika.”

Iye anati, “Zedi, iwo anali.”

Ine ndinati, “Ine ndimaganiza mpingo wa Katolika sunasinthe?”

Iye anati, “Iwo sunatero.”

266 Ine ndinati, “Ndiye nchifukwa chiani Petro anati, ‘Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu’? Ndipo inu mukuti uyo anali . . .kuti iye anali papa?”

267 “Eya.”

268 “Ndiye nchifukwa chiani inu mumabatiza mu dzina la ‘Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera’? Ndipo iye ankawamiza, ndipo inu mumawakonkha. Tsopano nchiani chinachitika?”

269 Iye anati, “Koma, inu mukuona,” anati, “mpingo wa Katolika uli nayo mphamvu yochita chirichonse chimene iwo ukufuna kuti uchite.” (nhu)

270 Ine ndinati, “Ndipo inu mukuwacha ophunzira Akatolika?”

271 Iye anati, “Eya.”

272 Ine ndinati, “Bwana, ine ndiri nalo la Josephus, ine ndiri nalo *Bukhu la Foxe la Ofera*, ine ndiri nalo la Pemberman la *Early Ages*, ine ndiri ndi *Two Babylons* la Hislop, mbiri zamakedzana kwambiri zomwe ziripo mu dziko, ndisonyezeni ine mmenemo pamene mpingo wa Katolika unayamba wadzozedwapo kapena unayamba wabwera mu bungwe . . .zaka sikisi handiredi itachitika imfa ya mtumwi wotsiriza.”

“O,” iye anati, “ife timakhulupirira zomwe mpingo umanena.”

Ine ndinati, “ine ndimakhulupirira zomwe Baibulo limanena.” Mwaona?

“Chifukwa,” iye anati, “Mulungu ali mu mpingo Wake.”

273 Ine ndinati, “Mulungu ali mu Mawu Ake.” Ndipo ine ndinati, “Ngati . . .” Iye anati . . .Ine ndinati, “Baibulo silimanena kuti Mulungu ali mu mpingo Wake, koma Baibulo limanena kuti Mulungu ali mu Mawu Ake. ‘Pachiyambi panali Mawu ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu; ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndiko kulondola. Ine ndinati, “Mulungu ali mu Mawu Ake.”

274 Iye anapitirirabe ndipo anakanena izo. Iye anati, “Chabwino, ife sitingamatsutsane,” anati, “chifukwa inu mumakhulupirira mu Baibulo, ine ndimakhulupirira mu mpingo.”

275 Ine ndinati, “Ine ndimakhulupirira kuti Baibulo ndilo Mawu owuziridwa ndi Mulungu ndipo mulibe kutsutsana kumodzi mu Ilo. Ndipo Ilo ndi Mawu a Mulungu, madongosolo Ake Amuyaya kwa mibadwo yonse yokudza. Iye anati, ‘Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma Mawu Anga sadzatha.’ Ndiko kulondola. Ine ndimawakhulupirira Mawu.”

276 Iye anapita uko kwa Akazi a Frazier. Iye anati, “Akazi a Frazier, kodi inu mungalembe pa chikalata apa kuvomereza kuti mtsikana wanu akhoza kukhala membala wa mpingo wa Katolika?”

277 Iye anati, “Ine kulibwino ndiyende naye mpaka ku manda.”

278 Anati, “Manyazi pa inu.” Anati, “Inu mukuyenera kukhala othokoza kuti msungwana uyo akubwera kuchoka mu zachabechabe izo, kudzalowa mu mpingo wa Katolika.”

279 Anati, “Bwanji ngati akanakhala ali msungwana wanu atabwera ku mpingo wanga, inu mukanati chiani pa izo?”

280 “O,” iye anati, “izo nzosiyana.”

281 Anati, “Ayi, siziri.” Iye ankadziwa kuti anakhala ali kwinakwake pamene iye ankasiyana ndi mkazi wamng’ono uyo kumeneko. Iye anadziwa kuti iye anakhala ali kwinakwake. Iye anati, “Tsopano, khomo lomwelo latseguka lomwe inu munalowa nalo.”

282 Mwaona, ndiyo njira yake. Musati inu muziponderezedwa, inu simukusowa kuti muziponderezedwa. Ngati Mulungu ali ndi inu, n’dani yemwe angakutsutseni inu? Kulondola! Vuto lake pa izo lero, inu muli ndi nsana wazokhumba mmalo mwa fupa lapa nsana. Ziimirani za Mulungu ndi zolondola!

283 Mzimu Woyera womwewo umene unabwera pa atumwi awo ndi mmbuyo mu mibadwoyo, ukadali mu Mpingo Wake lero, kwa iwo omwe Mulungu akudziululira Yekha. “Osati iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.” Ndi Mulungu, mwa kusankha Kwake, amawabweretsa anthu ndi kuwatsegula maso awo. Inu simungakhoze konse kuziwona Izo, ndinu akhungu, ndipo simukadakhoza kuziwona izo konse kupatula Mulungu atatsegula kumvetsa kwanu. Baibulo linati ndinu ‘akhungu,’ ndipo inu simungakhoze kupenya. Palibe kufunikira koti inu muziyesera. Ndi maphunziro onse, usikolala umene inu mungakhoze kuupeza, inu musingopitiriza kukhala akhungu moonjezera.

284 Tsopano, inu a Mpingo wa Khristu pano, inu mumayankhula pamene Baibulo likuyankhula, ndi kukhala chete pamene liri chete, nanga bwanji zina za Izi? Inu muli chete kwambiritu pa Izo. Kulondola.

285 Mwaona, izo zimatengera Choonadi choululidwa mwauzimu. Ndiye Mulungu amatsika ndi kudzadziulula Yekha ndi kutsimikizira Izo kuti ndi Choonadi. Amen! Inu mukumukonda Iye? Chomwechonso ine ndiri. Amen!

286 Chabwino, nonse inu Amethodisti mukufuna kuti mugwirane chanza ndi Abaptisti tsopano? Inu Apresbateria?

287 “Tsopano,” inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mukuwachotsa mu chiyanjano Abaptisti ndi Apresbateria omwe samaba- . . .”

288 Ayi, bwana, ine sindiri. Ine ndikuwatenga iwo ngati abale anga. Mwamtheradi! Ine sindisamala ngati inu muli osabatizidwa nkomwe, ngati inu munabatizidwa mu dzina la “Rozi la Sharoni, Kakombo waku Dambo, ndi Nyenyezi ya Mmawa,” izo sizikanakhala . . . izo zikananakhala chimodzimodzi basi ngati “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Maudindo atatu chabe. Iye anali Rozi laku Sharoni. Anali Iye? Kakombo waku Dambo, Nyenyezi ya Mmawa, zonse izo. Zedi, Iye anali. Chinthu chimodzi chokha kapena china. Koma pano pali chomwe chiri: njira yolondola ya Lemba ndi mu Dzina la Yesu Khristu. Ngati inu mukufuna njira ya Mwamalemba, ndizo ndendende. Ndiyo njira yolondola.

289 Tsopano, ngati inu munabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, . . .” mukumverera ngati kuti izo ziri bwino, ameni. Ngati liri yankho labwino kwa Mulungu la ku chikumbumtima chabwino kwa Mulungu, ameni. Zipitirirani nazoni, mwaona.

290 Koma monga momwe ine ndikukhudzidwira, monga mwa gawo langa, ngati inu mukanati mundifunse ine, kuti, “M’bale Branham, kodi ine ndikuyenera ndibatizidwe kachiwiri?” Ine ndikanati, “Inde,” kwa gawo langa.

291 Mkazi wamng’ono anabwera kuno tsiku lina, anati, “Ambuye andiitana ine kuti ndikhale mlaliki.” Ine sindinazikhulupirire izo, mosachuluka kuposa momwe ine ndikanakhulupirira k—kuti iye angalumphere pamwamba pa mwezi. Ndipo iye . . .

292 Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino kwambiri, mlongo.” Ine ndinati, “Kodi ndinu okwatiwa?”

“Inde.”

“Muli ndi ana awiri?”

“Eya.”

Ine ndinati, “Nchiani chomwe . . . Kodi amuna anu ndi opulumtsidwa?”

“Ayi.”

Ine ndinati, “Kodi inu muchita naye chiani iye?”

“Ndizimusiya iye kunyumba.”

293 Ine ndinati, “Iyo ndi nyambo yopambana yomwe Mdierekezi anayamba wakhalapo nayo. Ndinu mkazi wokongola pa kuyamba pomwe, ndipo inu mukazembera kwina uku mu ntchitoyi, inu mukhala nyambo yachizolowezi ndi chandamale cha Mdierekezi. Ndipo mwamuna wanu, ali kunyumba, mwamuna wamng’ono, ndipo inu mukamamusiya iye ndi ana

awiri awa; iye ayamba kuthamanga ndi mkazi wina, ndipo ana awa adzakhala ndi bambo wina limodzi la masiku awa.” Ine ndinati, “Malo oyamba, ngati Mulungu akanamuitana mkazi, Iye akanakhala akuwatsutsa Mawu Ake.” Ine ndinati, “Tsopano, ngati inu mukufuna kutero, izo ziri bwino.” Ine ndinati, “Tsopano, kuzindikira za mumtima, inu mukuti Ambuye wakupatsani inu kuzindikira za mumtima. Kodi inu mukufuna kuti mupite pa nsanja apo ndi kukaziyesa izo?”

²⁹⁴ Iye anati, “Inde.” Ndipo inu mukuwona zomwe zinachitika.

²⁹⁵ Inu mukuona, ndi kutengeka. Izo ziyenera kuti zizibwera ku Mawu. Ngati izo siziri mu Mawu, ndiye si zolondola. Ine sindikusamala chomwe zotengeka zanu ziri, izo si zolondola. Amen! Izo zikumveka bwino. Amen!

²⁹⁶ Chabwino:

Tiyenda nkuwala, kokongola,
Mame achifundo chowala;
Kuwale usana ndi usiku,
Yesu, kuwala kwa dziko.

Oyera lalikirani,
Yesu, kuwala kwa dziko;
Mabelo Akumwamba alire,
Yesu, kuwala kwa dziko.

Tiyenda nkuwala, kokongola,
Mame pang’ono . . .
Kuwale usana ndi usiku,
Yesu, kuwala . . .

²⁹⁷ Tsopano ine ndikufuna aliyense atembenuke apo ndi kugwirana chanza, ku mbali zinai, ndi aliyense tsopano, pamene ife tikuimba iyi kachiwiri:

Tiyenda nkuwala, kokongola, (ameni)
Mame achifundo chowala;
Kuwala usana ndi usiku,
Yesu, kuwala kwa . . .

²⁹⁸ Kodi inu mukuwakonda Achimethodisti? Nenani “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni”—Mkonzi.] Abaptisti? Achipresbateria? Akatolika? A . . . O, inu mukuwakonda iwo onse? Nenani “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tiyenda nkuwala, koko- . . . (tikugwirana
manja, pamene ife tikupita)
Mame achifundo owala;
Kuwale usana ndi usiku,
Yesu, kuwala . . .

²⁹⁹ Ife tisanaimbe nyimbo yobalalikira . . . Tsopano, ndi zotheka kuti ine ndidzakhalanso ndiri pano Lamlungu. Tsopano, zikatha izo ine sindibwereranso mpaka ikatha Khrisimasi. Mwaona, chifukwa ine ndikupita ku Michigan, kuchokera ku Michigan

ku Colorado, kuchokera ku Colorado waku Idaho, kuchokera ku Idaho mpaka ku California, ndipo ife tidzabwerera. Ndipo ndikotheka (ine ndikufuna inu muzindipempherera ine) ine ndikakhala ndiri ku Waterloo, Iowa, kuyambira pa Januwale twente-foro mpaka Febuwale pa thuu. Mwaona, ku bwalo lalikulu uko, ine ndangolandira kumene kuitanako kanthawi kapitako, ndipo ine ndiri nazo kuyambira tsopano mpaka Lamlungu kuti ndizipempherere. Mwaona, ku Waterloo, Iowa, komwe kuli pafupiko tsopano.

³⁰⁰ Koma tsopano, kumbukirani, zimvetserani ku kulengeza kwa m'bale naini koloko, Loweluka mmawa. Ife timuimbira iye ndi kumudziwitsa iye. Ndipo apo padzakhala pali pa WLRP, oyimba anai a Neville naini koloko, Loweruka mmawa. Ife tidza. . . Ngati i—ine sindikwanitsa kuwatenga iwo, M'bale Neville adzatsirizitsa mafunsowa. Mungadzatero inu, M'bale Neville, Lamlungu mmawa? [M'bale Neville akuseka ndi kuti, “Kulamulira kwakukulu.”—Mkonzi.] Chabwino, penyani, ngati inu mudzalowa mu vuto, ine ndidzathamanga nanu. Iye adzayang'ana. Chabwino.

³⁰¹ Chabwino:

Tenga dzina la Yesu nawe,
Wachisoni ndi tsoka;
Lidzakusangalatsa iwe,
Litenge konse upita.

Dzina lofunika, kukoma kwake!
Chiyembekezo cha amdziko;
Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma
kwake! (kukoma kwake)
Chisangalalo cha Kumwamba.

³⁰² Tsopano, ngati inu mukufuna kumudziwa Mb'aptisti yemwe amakhulupirira mu kufuula, uwo ndi mtundu wa kufuula womwe ine ndimaikhulupirira. Mayi wachikulire uyo atangokhala apo, ndipo Mzimu unadza pa iye. Iye anayamba kukuwa, iye sakanakhoza kuzigwira izo, iye anabwerera mmbuyo ndi kukamukumbatira mwana wake wamkazi. Ndi momwe ine ndimakondera kuziwona izo. Amen. Ndiko kumverera kwenikweni kwabwino, kwa mtundu wachikale, kokhudza mtima. O, mai, woyera wachikale—wokhwima, wachikulire, wokucha, wokonzeka kuti azipita kwawo ku Ulemerero. Akungodikirira kuitanidwako, inu mukuona, akungokhala ndi nthawi yodabwitsa.

Chabwino, M'bale Neville tsopano, chirichonse chomwe iye akufuna kuti achichite.



Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org